MPHAMVU YA MULUNGU YOSANDULIZA

Tucson, Arizona USA
SEPITEMBALA 11, 1965

1 Zikomo inu, M'bale. ["Ndithudi ndi mwayi weni weni kuti M'bale Branham amabwera pafupi pafupi kwambiri ku Phoenix. Ine ndikuganiza kuti iye amabwera ku Phoenix mochuluka kuposa kwina kuli konseko. Ndipo ife tikufuna kuti iye azibwerabe, nthawi yonse pamene ine ndiripo, mulimonse. Mulungu akudalitseni inu, M'bale Branham."] Zikomo, zikomo inu, M'bale Williams.

Mmawa wabwino, abwezi, Ine....

Banja la a Shakarian, M'bale Williams ndi Mlongo Williams ndi ochuluka a iwo kuno akudziwa za chimenecho. Ine ndinaziwona izo mmasomphenya, pafupi zaka ziwiri mpaka zitatu iye asanayambe kudwala, ndipo izo zinadzachitika. Ndipo chaka chatha pamene ife tinali kuno, ine ndikukhulupirira umo munali mu Januwale, ku msonkhano waukulu, inali nthawi pamene wansembe uja (dzina lake ndi ndani? Ine ndaiwala dzina lake tsopano) anali kuno. [Winawake akuti, "Stanley." - Mkonzi.] Stanley, Bishopu Stanley, wochokera ku mpingo wa Katolika. Inu mukukumbukira pamene iye anandibweretsera ine Baibulo, inu mukudziwa, ndipo iye analankhula ndi ine. Analipo angapo amalosera, "Mwana wanga wamkazi, iwe wachiritsidwa." Ndipo iye ankadziwa kuti masomphenya anali atanena kuti iye sakhala bwino. "Iye anali woti afa pakati pa 2 ndi 3 koloko m'mawa." Mukukumbukira zimenezo? [Wina akuti, "Inde." - Mkonzi.] Kotero, 2 kapena 3 koloko.

2 Ndipo ine sindikanakhoza kumuuza Demos. Ndipo komabe ine ndinawauza amai ake omupeza, uko komwe mu chipinda, patsidya kuno. Ine ndinati, "Iye sakhala bwino."Akazi a Shakarian."

Anati, "Chabwino, aliyense akulosera."

Ine ndinati, "Ndithudi, ineyo ndikhoza kukhala kuti ndikulakwitsa, ine mwini, koma ine ndinanena izo. Iye sakhala bwino." Ine ndinawawuza ambiri a iwo, pafupi zaka zitatu zapitazo, "Ine ndinamuwona iye akuthamangira moyo wake, ndipo iye anapita mu bedi. Ndipo iye anakweza manja ake ndi kumafuulira kwa ine, monga choncho. Ndipo Ine - ine sindinakhoze nkomwe kumufukira iye. Ndipo kenako ine ndinamuwona iye akufa. Ndipo ine ndinayang'ana, ndipo apo panali china chake, apo panali watchi ndipo iyo inati ndi china chake pakati pa 2 ndi 3 koloko."

Ndipo kotero bishopu anati, "Chabwino, ine ndingopenya ndi kuwona momwe ziti zifikire pochitika." Kotero, izo zinafika pochitika.

3 Ife ndithudi tikupepesa. Ine ndikumverera kuti mpingo wataya munthu wopambana, mwa Mlongo Florence Shakarian, Koma.. iye anali woyimba wopambana, iye anali mkazi wodzazidwa ndi Mzimu.

Ine ndinali ndi amayi ake; amayi ake anali mmodzi wa olembelana nawo woyamba omwe ine ndinali nawo ku Gombe Lakumadzulo, pamene amayi ake anachiritsidwa. Pamene madotolo… Iye anali atakomoka, ndipo atatupa yense. Ndipo kotero - dotokotala yemwe anali uko anandiuza ine, anati, "Tsopano mukakhale chete kwenikweni pamene inu mudzikapemphera. Musakapange phokoso lochuluka. Mayiyu akufa."

Ine ndinati, "Inde, bwana."

Ndipo iye anati, ndiye, anangopitiriza kumandiuza ine. Ndipo, mwakuti, ine ndinalibe nkomwe mwayi woti nditsegule kamwa yanga, mokhala ngati.

4 Chotero, anali M'bale Demos anandiuza ine kuti ndipitirire ndi kupita m'mwamba ndi kukamuwona iye.Chotero, ine ndinapita m'chipinda m'mwamba. Ndipo Florence anali atagwada pansi, ndiye msungwana wamng'ono wokongola, ndi akazi ena ambiri. Ndipo ndinapita apo ndi kukapempherera iye, ndipo ndinachinena icho. Ndipo iye anali atakomoka. Ndipo ndinamuuza iye kuti adzukaponso. Ndipo iye anatero. Zaka zingapo mtsogolo, iye anadzafa.

Ndipo tsopano Mulungu amayankha mapemphero athu. Ndipo ife tikudziwa zimenezo, ife timakhulupirira kuti ife tonse tinabwera kuno mwa chifuniro cha Mulungu, ndipo ife tidzachokapo mwanjira yomweyo. Mmodzi ndi mmodzi, ife tidzawoloka aliyense khomo limenelo. Ndipo ndicho chifukwa ife tiri pano m'mawa uno, titasonkhana limodzi mu Christian Business Man's Fellowship iyi, ndi kuti tidzayankhule za zinthu izi, ndi kuzikonzekera izo, chifukwa ife tikudziwa kuti izo zidzabweradi motsimikiza.

5 Tsopano Mlongo Florence ndi mayi wam'ng'ono, usinkhu wa zaka makumi anayi ndi ziwiri, M'bale Williams wandiuza kumene ine, ndi wam'ng'ono kwambiri. Koma asanati iwo, iye asanadziwe kuti iye anali ndi matenda awa, bwanji, ine ndinawona masomphenya a iye ndipo anandiuza ine zotsatira zake. Ndiye, izo zikanakhala. Mulungu amadziwa zonse za izo, ndipo iye anamuwona Yesu m'chipinda iyeyo asanachokemo. Ife sitikufuna basi kuti timupempherere iye, chifukwa ife tachita zimenezo mochuluka kwambiri. Ife tikungofuna kuti timuthokoze Mulungu chifukwa cha moyo umene unali pakati pathu, umene umatikondoweza ife tonse, monga mlongo Shakarian.

Ndipo ife tikufuna kuti timupempherere M'bale Demos, Mlongo Rose. Ndipo kumbukirani, iwo akhala nako kumenyedwa kolimba mu moyo wawo, zathazi…. Ndi bambo ake, ndi mlongo wake tsopano mwake…. Zaka zathazi. Koma, ndi, eya, kuchepera, miyezi khumi; ndi mlongo, Mlongo Edna, nayenso.

6 Kotero, ine ndikudziwa momwe ndingamvere naye chisoni M'bale Demos. Ine ndinali nawo bambo, m'bale, mkazi, ndi mwana, omwe anapita motalikirana masiku pang'ono, chotero Ine - ine ndikudziwa momwe iye akumverera m'mawa uno. Iwe umadziwa kokha pamene iwe uimapo mu nsapato zawo, ndi pamene iwe umadziwa momwe ungamverere nawo chisoni.

Ndipo… [Zowulutsira mawu zikukuwa - Mkonzi.] Ine ndinachita izo mwiniwanga. Mundikhululukire ine. Ine ndinagunda kanthu kakang'ono pano penapake, ndi dzanja langa. Chotero ine ndiri - ine ndikupepesa ndinapokosera mochuluka kwambiri, ndipo sindimatanthuza kutero.

Chotero tiyeni ife tiime tsopano pamene ife…. Ngati inu mungathe, ngati ziri…. Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

7 Atate Akumwamba, ife tasonkhana pano m'mawa uno kuti tidzakupembedzeni Inu, ndi kudzakupatsani Inu mathokozo ndi matamando, chifukwa chotitumizira Yesu Muomboli wathu, kuti tiri ndi chiyembekezo moyo uwu utatha, kuona kuti ndi zosatsimikizika kuti ife tidzikhala kuno nthawizonse. Ndipo, Atate, powona zikhalidwe zomvetsa chisoni zomwe matupi awa angalowemo, ife tiri okondwa ife sitikusowa kuti tizikhala kuno nthawi zonse. Inu munapanga njira yothawira, podutsa mu chigwa cha imfa.

Ndipo, Atate, ife tiri oyamikira kwa Inu m'mawa uno, chifukwa cha moyo wa mmodzi yemwe anaima ndi ife, mocheperapo chaka, akuimba matamando Anu; Mlongo Florence Shakarian, monga ife timamudziwira iye. Ndipo Inu munatiuziratu ife kale patali, ngakhale zaka, kuti izi zinali zoti zidzachitika, kuti izo zisadzati zidzakhale zodzidzimutsa kwambiri kwa ife. Ndipo ife tikudziwa kuti zomwe Inu mumanena ndi zoona.

Ndiyeno Mawu Anu amati, "Munthu wobadwa mwa mkazi ndi wodzadza ndi masiku apang'ono ndi wodzadza mavuto." Ife tikudziwa kuti izo nzoona, nazonso, Ambuye. Ife tikudziwa ife tonse tiyenera kubwera kudutsa muchigwa chimenecho.

Kotero ife tikukuthokozani inu chifukwa cha moyo wake umene unali kuno pa dziko lapansi. Ndipo tikukhulupirira mwa chikhulupiriro, kuti tsopano m'mawa uno, iye wapita kuchoka mu nyumba ya tizilombo yomvetsa chisoni ino, wakalowa mu thupi laulemerero lomwe silingakhoze konse kudwala. Ndi luso lake la kuimba, ndi liwu lomwe iye anali nalo, ndi mzimu wake wolemera kwambiri mu chisomo ndi Khristu! Kuti iye akanakhoza kubwerera m'mawa uno, iye sangachite izo mwanjira iliyonse; iye angasowe kuti adutse mu zonse izi kachiwiri. Zimene, tsopano izo zatha, iye ali ndi amayi ake ndi adadi ake. Iwo amuitana mwana wawo kunyumba. Kotero, ife tikukuthokozani Inu.

8 Ife nafenso tikufuna tipemphere chitonthozo, kwa M'bale wathu Shakarian, m'bale wathu wokondedwa, podziwa - moyo umene iye wakhala, ndi mazunzo omwe iye akudutsamo mu masiku otsiriza ano, ndi momwe iye aliri; pomuona iye akukalamba, ndi tsitsi lake likuthothokamo, ndi mapewa ake akugwa, ndipo komabe kumayesera kuti akhalebe pa ntchito ya Mulungu. Mulungu, mumpatse iye mphamvu lero. Tikupemphera Mulungu, kuti Inu mupereke izo.

Kwa onse awo omwe asiyidwa ndi kupita kwake, ife tikupempherera wina aliyense. Ndipo mutilole ife, Ambuye, pamene ife tikulingalira za izi, tidzikumbukira kuti ife nafenso tiyenera tidzapite tsiku lina. Pamene ife tikukhala pamodzi pano muKukhalapo kwa Ambuye Yesu, ife tikanafunsa kuti Inu mubweretse izi mwatsopano ku kukumbukira kwathu. Ndipo mutilole ife tifufuze, monga izo zimakhalira, kapena titenge kufufuza kwa miyoyo yathu yomwe, kuti ife tikhale pansi pa Magazi ndi mu chikhulupiriro. Perekani izi, Ambuye.

9 Tsopano pamene ine ndikuyesera pansi pa zochitika izi kuti ndibweretse uthenga waung'ono kwa anthu, lero, ine ndikupemphera kuti Inu mundithandize ine, Ambuye. Ndilimbitseni ine, pakuti Ine - Ine - ine ndikuzisowa izo, Ambuye. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mupereke izo. Ndipo mulole china chake chinenedwe chomwe chiti chingokulemekezani Inu. Ndipo ngati pangakhale aliyense pansi pa kumveka kwa liwu lathu m'mawa uno, yemwe sanakonzeke kuti akomane nalo ora lomwe liri patsogolo pawo, mulole iyi ikhale nthawi yomwe ati adzipereke kwa Iye Yemwe anati, "Ine ndine Njira, Moyo, Choonadi," ndiye Ambuye wathu Yesu Khristu. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina Lake. Ameni.

(Inu mukhoza kukhala.)

10 [Winawake pa guwa akuyankhula ndi M'bale Branham - Mkonzi.] M'bale pano akufuna kuti adziwe ngati aliyense akukhoza kumva bwinobwino. Iye wayatsa zoyankhulirapo ziwiri. Kodi izo ziri bwino? Kodi inu mukukhoza kumva? Kwezani m'mwamba manja anu ngati inu mukukhoza. Kodi inu mukukhoza kumva? Kwezani manja anu. Chabwino.

Ine ndikupepesa kuti ife tiribe malo okhalapo kwa aliyense m'mawa uno. Ndipo ife tikudalira kuti ine sindikhala pano motalika kwambiri, zongokwanira basi kuti mwina mwake zitibweretse ife ku kuwerenga kwa Mawu; kuti Ambuye Mulungu alemekeze Mawu Ake omwe ali kuwerengedwa, ndipo atipatse ife za chisomo Chake, kuti ife tikhoze kumutumikira Iye ndi icho.

11 Tsopano ine ndinauzidwa ndi Billy Paul, m'mawa uno, kuti zikhoza kukhala zotheka kuti ife tidzayankhule Lamlungu lotsatira ku Grantway Assembly of God, mu Tucson. Ngati alipo aliyense pano wochokera ku Tucson, ine mwina sindingathe kuonana nanu sabata imeneyi, ine ndidzakhala ndiri ku Grantway Assembly of God, Lamlungu likudzali.

Kotero tsopano ife tangobwera kumene kuchokera uko kum'mawa, ndipo ine ndakhala ngati ndadzitopetsa ndekha pang'ono, pa kudya mopitiriza, ndi chifundo chopitirira cha anthu a ku mapiri uko. Ndipo - ndipo ine ndinadwala, chotero ine sindinamverere bwino sabata ino. Kotero, inu mudzindipempherera ine.

12 Ndi…Winawake akuti, "Aposamu wochuluka kwambiri." - Mkonzi.] Inu mukuti chiani? ["Aposamu wochuluka kwambiri."] M'bale Carl Williams ali ndi kachitidwe kosangalatsa, ndipo ine ndikuganiza ife tikuzisowa izo pakali pano, iye anati, "Aposamu wochuluka kwambiri." Ine sindikudziwa za izo, M'bale Carl, koma agologolo ochuluka kwambiri. [M'bale Branham akuseka.]

Kotero inu mukafuna kuti mumupempherere winawake m'mawa uno, bwanji, Ine -ine ndithudi ndiyamikira ngati angakhale ali ena a mapemphero anu kwa ine, chifukwa Ine ndikusowa iwo.

Tsopano ife tikufuna kuti tipite mofulumira mu Mawu.

13 Ndipo ine sindikufuna kuti ndikusungeni inu pano motalika kwambiri, chifukwa ine ndikukhulupirira kuti pali kulumikizana kwa telefoni kudutsa mu fukoli, pa izi m'mawa uno, kukupita ulendo wonse kuchokera ku Gombe la Kumadzulo kupita ku Gombe la Kum'mawa, kuchokera Kumpoto ndi kummwera. Magulu ambirimbiri, ali nako kulumikiza kumeneku monga inu nonse mwakhala munali nako kuno kuchokera ku kachisi. Izo zalumikizidwanso ku Phoenix, kuti kulikonse kuli msonkhano, izo zikufika kumene umo…. Ndipo iwo akusonkhana mu tchalitchi ndi m'manyumba, ndi zinthu monga choncho, zikudutsa mu mpweya wa mawu wabwino kwambiri. Iwo amati izo zikukhala bwino kwambiri kuposa kuulutsa. Ndi kulumikiza kwa telefoni, iwo amaika cholandirira kapena cholankhulira, kapena chiriri chonse chomwe icho chiri, mu chipinda. Ndipo iwo… Mkazi wanga anati, akubwera kuchokera ku Indiana sabata yatha, akupita ku Tucson, izo zinangokhala chimodzimodzi ngati waima kumene mu chipindachi. Kotero ife tikupemphera kuti Mulungu awadalitse onse awo omwe ali pa kulumikazana m'mawa uno, kuli konse komwe iwo ali. Uko ku New York tsopano uko kukhala kuli, o, madzulo, ndi nthawi zosiyana pamene zikudutsa fukoli.

14 Tsopano mu Buku la Aroma, mutu 12, ndipo ndime ya 1 ndi 2, ife tikukhumba - tikukhumba kuti tiwerenge Lemba ili.

Ine ndikukupemphani inu chotero, abale, mwa zifundo za Mulungu, kuti inu mupereke matupi anu ngati nsembe zamoyo, zoyera, ndi zovomerezeka kwa Mulungu, komwe kuli kupembedza kwanu koyenera.

Ndipo musakhale inu ofaniziridwa ndi dziko lino: koma inu mukhale osandulika mwa kukonzanso kwa malingaliro anu, kuti inu mukhoze kutsimikizira chomwe chiri chifuniro chabwino, ndi changwiro… chabwino, chovomerezeka, ndi changwiro, cha Mulungu.

Tsopano, ngati Ambuye alola, ine ndikufuna kuti nditenge phunziro langa m'mawa uno, pa: Mphamvu Ya Mulungu Yosanduliza.

Kuti inu musakhale muli ofaniziridwa ndi dziko lino: koma mukhale…osandulika mwa kukonzanso kwa malingaliro anu, tsopano, ndi kutsimikizira icho chomwe chiri chifuniro chabwino, changwiro, ndi chovomerezeka, cha Mulungu.

15 Ndi nkhani yakale yodziwika yomwe ambiri a abusa anu aigwiritsa ntchito konse kudutsa mu nthawi yanu. Iyo yakhala ikugwiritsidwa ntchito kuyambira pomwe Iyo inalembedwa. Komabe, chinthu chimodzi chokhudza Mawu a Mulungu, Iwo samakalamba konse, chifukwa Iwo ndi Mulungu. Iwo samakalamba konse. Kupyola mu kam'badwo kalikonse tsopano, kwa pafupi, zaka zikwi ziwiri nd mazana asanu ndi atatu, kapena mwabwinoko, Mawu awa a Mulungu akhala akuwerengedwa ndi anthu, ansembe, ndi ena otero, ndipo Iwo, sakukalambabe. Ine ndakhala ndikuwawerenga Iwo ine mwini, kwa zaka zina makumi atatu ndi zisanu. Ndipo nthawi ili yonse yomwe ine ndimawawerenga Iwo, ine ndimapeza china chake chatsopano chomwe ine ndinachilambalala pa nthawi yoyamba. Chifukwa, Iwo ndi odzozedwa, Iwo ndi Mulungu mu maonekedwe a zolembedwa. Mwaona, Iwo ndi zikhumbo za Mulungu zikuyankhula, ndipo izo zinaikidwa pa pepala.

16 Nthawi zambiri, munthu amati, "Chabwino, tsopano, munthu analilemba Baibulo ili." Ayi. Baibulo limati, Ilolo, kuti Mulungu analemba Baibulo. Ilo ndi Mawu a Mulungu. Ndipo Iwo sangakhoze konse kulephera. Yesu anati, "Miyamba ndi dziko la pansi zidzalephera, zidzachoka, koma Mawu Anga sadzalephera konse."

Ndipo Iwo sangakhoze kulephera, ndipo pokhala Mulungu, chifukwa Iwo ali gawo la Iye. Ndiyeno inu pokhala mwana Wake wamwamuna ndi wa mkazi, inu muli gawo la Iwo, ndipo izo zimakupangitsani inu kukhala gawo la Iye. Kotero ndi chifukwa chake ife timabwera kudzayanjana limodzi mozungulira Mawu a Mulungu.

17 Tsopano mawu awa oti kusandulika, ine ndinawayang'ana iwo mu bukhu lotanthauzira mawu, dzulo. Pamene, ine ndinali pafupi kutaya kulondola kwa nthawi yomwe ine ndimayenera kuti ndidzakhale ndiri kuno, pamene ine ndimaifunafuna nkhaniyi, ndipo ine ndinapeza mawu awa, kapena nkhani iyi, kani, Lemba. Ndipo mu bukhu lotanthauzira mawu ilo limanena kuti ndi "china chake chomwechasinthidwa." Chirichoti "chisinthidwe." Kusandulika, "kupangidwa mosiyana ndi chimene icho chinali." Icho chakhala chiri, "Khalidwe lake ndi chirichonse chasinthidwa mwa icho," kusandulizidwa.

18 Ndipo ine ndimaganiza m'mawa uno, mu Genesis 1. Dziko lino linali lopanda maonekedwe, ndipo ilo linali lopanda kanthu, ndipo m'dima unali pa dziko lapansi; panalibe kanthu koma chisokonezo chathunthu. Ndipo pamene dziko lino linali mu chikhalidwe chimenecho, Mzimu wa Mulungu unkayenda pamwamba pa madzi, ndipo chithunzi chonsecho chinasinthidwa; kuchoka ku chisokonezo chathunthu, kukakhala munda wa Edene. Iyo ndi Mphamvu yosanduliza ya Mulungu, yomwe ingakhoze kutenga chinachake chomwe sichiri kanthu ndi kupanga chinachake chodabwitsa kuchokera mwa icho. Mphamvu yosanduliza ya Mulungu!

19 Ndipo ife tikumva kuti, pa kuwerenga Malemba, kuti Mulungu anali ndi zisanu ndi chimodzi - zaka zikwi zisanu ndi chimodzi akupanga kukonzekera uku kwa Edene uyu. Tsopano, Iye mwina akhoza kusakhala kuti anali utali wotero; koma basi kungopenekera, ndi kuzitenga izo kuchokera mu Lemba pamene Iwo anati "tsiku limodzi kwa Mulungu, liri zaka chikwi pa dziko lapansi," izo ziri, ngati Mulungu akanati aziwerenga nthawi. Ndipo iwo amati zinali zaka zikwi zisanu ndi chimodzi zomwe Iye anali nazo pa kulipanga dziko lapansi, ndipo Iye anali atabzala pa dziko lapansi mbewu zonse zabwino. Apo panali basi chirichonse chiri changwiro.

Ine ndikuganiza, nthawi zambiri, ngakhale pamene otsutsa ayamba kuwerenga Buku la Genesis, iwo amayamba kulitsutsa Ilo, chifukwa izo zimawoneka kuti mowirikiza Ilo limangodzibwereza Lokha, kapena kukuponyerani inu kunja apa ndi apo.Koma ngati ife tikanati tingozindikira kwa mphindi, ife tisanalowe mu nkhani yathu, kuti, Mose anawona masomphenya. Ndipo Mulungu anayankhula ndi iye. Mulungu ankayankhula kwa Mose maso ndi maso, mulomo kwa khutu. Tsopano, Iye sankayankhula konse ndi munthu wina aliyense monga choncho, momwe Iye ankachitira naye Mose. Tsopano, Mose anali wamkulu, mmodzi wa aneneri aakulu onse. Iye anali choimira cha Khristu.

Ndipo tsopano Mulungu akhoza kulamkhula, Iye ali nalo liwu. Ilo lakhala likumvedwa. Mulungu akhoza kulankhula.

20 Ndipo Mulungu akhoza kulemba. Mulungu analemba Malamulo khumi ndi chala Chake Chomwe. Iye analemba pa makoma a - a Babeloni kamodzi, ndi chala Chake. Iye anawerama pansi ndipo analemba mu mchenga nthawi ina, ndi chala Chake. Mulungu akhoza kulankhula. Mulungu akhoza kuwerenga. Mulungu akhoza kulemba.Mulungu ali kasupe wa chisomo chonse ndi Mphamvu, ndi nzeru zonse za Umulungu, ziri mwa Mulungu.

Kotero chomwecho, podziwa izo, Iye ali Mlengi yekha yemwe alipo. Palibe Mlengi wina kupatula Mulungu. Satana sangakhoze kulenga, nkomwe, iye amangopotoza zomwe zalengedwa. Koma Mulungu ndi Mlengi Yekhayo. Chotero, Iye analenga ndi Mawu Ake. Iye anawatumiza Mawu Ake. Kotero mbewu zonse zomwe Iye anali ataziyika pa dziko lapansi, Iye anaziumba mbewu zimenezo ndi Mawu Ake Omwe, pakuti kunalibe kena kalikonse koti apangire mbewu nako. Iye anali atadziyika izo, ndipo izo zinali pansi pa madzi. Iye anangoti, "Pakhale ichi, ndipo pakhale icho."

21 Tsopano ife tikupeza kuti, nthawi zambiri, izo zimawoneka ngati Baibulo likudzibwereza kapena likunena chinachake chomwe Ilo silikunena. Mwa chitsanzo, mu Genesis 1 ife tikupeza kuti "Mulungu anamulenga munthu mu chifanizo Chake Chomwe, mu chifanizo cha Mulungu Iye anamulenga iye; mwamuna ndi mkazi Iye anawalenga iwo." Ndiyeno Iye akupitirira, ndipo zinthu zambiri zinachitika pa dziko lapansi.

Ndiye ife tinafika popeza kuti, panalibe munthu woti adzilima m'nthaka. "Ndiye Mulungu anamulenga munthu kuchokera mu fumbi la dziko lapansi." Uyo anali munthu wosiyana. "Ndipo Iye anapumira mzimu wa moyo mwa iye, ndipo iye anadzakhala solo ya moyo."

22 Munthu woyamba anali mu chifaniziro cha Mulungu, umene uli Mzimu. Yohane 4, amati, "Mulungu ndi Mzimu, ndipo iwo amene amupembedza Iye ayenera adzimupembeza Iye mu Mzimu ndi mu Choonadi." Koma Mulungu ndi Mzimu. Ndipo munthu woyamba, yemwe Iye anamulenga, anali munthu - wauzimu, ndipo iye anali mu chifanizo ndi m'mawonekedwe a Mulungu. Ndiyeno Iye anamuika munthu uyu mu mnofu, ndipo munthu anagwa. Koterono Mulungu anadzabwera pansi ndipo anadzakhala mu chifanizo cha munthu, kuti Iye adzakhoze kumuwombola munthu wakugwa uyo. Imeneyo ndi nkhani yeniyeni ya

Uthenga, mwa - mwa kulingalira kwanga.

23 Tsopano, Mulungu, mu zaka zikwi zisanu ndi chimodzi, anali atabzala mbewu zonse zodabwitsa izi, kapena Iye anali atayankhula Mawu Ake. "Izo zidzakhala ziri mwanjira iyi. Mtengo uwu udzakhala uli. Izi zidakhala ziri." Chirichonse chinali changwiro. Izo zinali zabwino basi. Ndipo Iye anailamulira ili yonse ya Mbewu zimenezo chimene zikanadzakhala, izo zikanamadzadzisintha zokha kukhala mbewu ya mtundu wake wa moyo umene Mawu a Mulungu anali atauyankhulira mwa izo kuti umayenera kukhala uli. Ngati iwo unali mtengo wa mgwalangwa, iwo unali woti udzibala mgwalangwa. Ngati iwo unali kanjedza, iwo unali woti udzibala kanjedza. Chifukwa, Mlengi wamkulu anali basi atangotumiza Mawu Ake, ndipo mbewu ya Mawu inali apo mbewu yeniyeni isanaumbidwe konse. Ndipo Mawuwo anapanga mbewuyo. Mwaona,

"Iye anapanga dziko kuchokera mu zinthu zomwe siziri kuwoneka." Mwaona, Iye - Iye anapanga dziko ndi Mawu Ake. Mulungu anayankhula chirichonse kuti chikhalepo.

24 Ndipo pokhala Mulungu, Mlengi, akuyankhula zinthu zonse kuti zikhalepo, ilo liyenera kuti linali dziko langwiro. Awo anali - malo okongola. Iyo inali pa - paradaiso yeniyeni pano pa dziko lapansi. Tsopano, monga, malo aliwonse ayenera akhale ali ndi likulu kwina kwake. Msonkhano waukulu uno uli ndi likulu, ndipo chaputala chino chiri ndi likulu, ndipo mpingo uli ndi likulu. Ndipo Mulungu ali nalo likulu. Ndipo chomwecho malo aakulu ano, fuko lomwe ife tiri kukhalamo, liri nalo likulu. Ndipo kotero Edene wamkulu uyu anali ndi likulu, ndipo likulu lake linaikaidwa mu munda wa Edene, kapena mu Edene, kum'mawa kwa kwake m'mundamo. Ndipo Mulungu Anaika pamwamba pa uwu, kuti azilamulira pa chilengedwe Chake chopambana chonse pano pa dziko lapansi, mwana Wake ndi mkwatibwi wa mwana Wakeyo, Adamu ndi Hava.

25 Mulungu anali Atate wa Adamu. "Adamu anali… mwana wa Mulungu," monga mwa Malemba. Iye anali mwana wa Mulungu. Ndipo Mulungu anamupangira iye womuthandizira, kuchokera mu thupi lake lomwe; mwinamwake nthiti kuchokera pamwamba pa mtima wake, kotero kuti iye azikhala wapafupi kwa iye, ndipo anamupangira iye womuthandizira. Iye kwenikweni sanali mkazi wake apabe, mosaposa momwe iye analiri mwamuna apabe; Iye anali atangoyankhula izo. Ndipo apo ndi pamene vuto linabwerera, Satana anamupeza iye Adamu asanatero. Kotero, awo anali basi Mawu Ake omwe Iye anawayankhula.

26 Ine ndikunena izo.. ine sindikufuna kuti nditaye nthawi yochuluka kwambiri pa zimenezo. Koma ena a inu mukhoza kusokonekera pang;ono, makamaka ena a anthu mu - uko kumwera, mukuwoneka ngati mumapeza kusokoneza pang'ono, pa Uthenga umene ine ndiri nawo wochokera kwa Mulungu lero, wa kwa anthu, uwo wa mbewu ya serpent. Ndipo ine ndipita kwathu, Ambuye akalola, limodzi la masiku awa, ku Jeffersonville. Ine ndikufuna pafupi uthenga wa ma ora asanu ndi limodzi, ndikukaziwongola zonse izo apo, mwaona, kuti ine ndidzadziyike izo mu mawonekedwe omwe inu mudzadziwe zomwe ife tikuzikamba. Ndipo ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndi zoona abasi monga izo zinaliri pamene Izo zinamuwona Mlongo wathu Florence iye asanapite zaka zingapo. Mwaona, ndi Choonadi.

Ndipo tsopano, ife.. mwina mwake izo sizimamvetsetsedwa.

27 Ngati wina wake akanabwera kwa ine, ndi china chake chosiyana, ine ndikanakhala ngati osachimvetsa icho, ine mwini. Ine sindikanafuna kuti nditsutse chimene aliyense anena. Ife sitili woti tizitsutsana wina ndi mzake. Ine sindiri wolakwa pochita izo; ine ndikuwathokoza Ambuye. Ine ndatsutsapo tchimo ndi kusakhulupirira; koma osati munthu payekha, mwaona, Ine - ine sindiri. Ife tiri - ife tiri abale ndi alongo, tikulimbikira, ife tikubwera mpaka kumene mlongo Florence anabwera dzulo mmawa, mwaona. Iye, ife, ife tonse tiyenera kubwera njira imeneyo. Ndipo si cholinga changa ku - kuti ndiziyesera kumutsutsa m'bale kapena mlongo yemwe sakanakhoza kugwirizana nawe. Ayi, zikhale kutali ndi ine kuti ndingachite zimenezo! Ine sindikuganiza kuti inu mudzapezako tepi yomwe ine ndinayesera kutchulapo dzina la aliyense. Chimene, ine ndamvererapo chimenecho nthawi kuti zambiri munthuyo akulakwitsa, koma izo ziri pakati pa iwo ndi Mulungu. Koma chimene chiri cholakwika, munjira ya tchimo ndi…. Ndipo kusamvetsetsana nthawi zina silimakhalanso tchimo nkomwe, ndi kusamvetsetsana basi kwa anthu. Ndipo I - ine ndikuganiza wina aliyense wa ife ali nawo ufulu wodzifotokoza ife eni pakumvetsa kwathu.

28 Tsopano Mlengi wamkulu uyu anali atamuika mwana Wake wolengedwa… Tsopano, Adamu anali mwana Wake woyamba wolengedwa. Yesu anali Mwana Wake yekhayo wobadwa yekha mwaona, Iye anali wobadwa yekha mwa mkazi. Koma Adamu anali wolunjika kuchokera m'dzanja la Mulungu, mwa kulenga. Tsopano likulu, ndi Wake - mwana Wake ndi Mkwatibwi wa mwana Wake woyang'anira pa zonse, izo zinkawoneka zangwiro kwambiri. Uko kunali m - munthu, mutu wa zonsezo, mwana Wake Yemwe ndi mkwatibwi wake.

Ndipo mbewu iliyonse inali yangwiro, kanjedza, ndi migwalangwa, ndi udzu, ndi mbalame, ndi zinyama. Ndipo chirirchonse chinali mu dongosolo la ngwiro ndi Lamulo la Mulungu, "Musasinthe chikhalidwe chanu. Zizibala za mtundu wake, mbewu iliyonse! Mgwalangwa, iwe usati udzapotezedwe kukhala mtengo wa papaya." Mwaona? "Kanjedza usati udzapotozedwe konse kukhala chinachakenso. Koma mbewu iliyonse monga mwa mtundu wake!"

29 Ndipo Iye anaziyang'anira izo kudutsa mu nthawi. Ndipo Iye anali atayankhula Mawu. Ndipo Mphamvu Yake yaikulu yolenga inali itapanga zinthu izi zomwe zinadzapo, ndipo ngakhale mwamunayo ndi mkazi. Ndipo iwo anali mutu chifukwa iwo anali…. Iwo anali apamwamba kwa mitundu ina yonse. Ndipo Iye anawaika iwo nawonso pansi pa chisamaliro cha chinthu chofanana chimene Iye anayikapo mitengo, nyama, ndi zina zotero: Mawu Ake. Iwo azikhala mwa njira iliyonse, aziswa Mawu amenewo. Iwo asayerekeze mwanjira iriyonse kuphwanya Mawu amenewo. Iwo azikhala pamenepo. "Musadzatenge konse chirichonse kuchokera kwa Iwo, kapena kuwonjezera chirichonse kwa Iwo! Inu muzikhala moyo ndi Mawu awa." Ndipo bola ngati chirengedwe chimenecho chikanati chidzikhalabe monga choncho, Mlongo Shakarian sakanati akhale atapita m'mawa uno, bola ngati izo zikanati zikhalebe monga choncho, chuma chachikulu cha Mulungu! Ndi chimene ife tikukhulupirira kuti tikubwererako. Ife tikubwerera ku kamalo ako, malo amenewo.

Kumene m'mawa wa chisanu ndi chiwiri uwo, pamene Mulungu anayang'ana pa izo zonse, ndipo Iye anati, "Ziri bwino. Ine - Ine ndikukondwera nazo izo. Eya, Ine - Ine - Ine ndiri wokondwa kuti Ine ndazichita izo. Ndipo zonse izo tsopano ziri pansi pa ulamuliro. Ndipo Ine ndaika chidaliro mwa mwana Wanga ndi mwa mkazi wake, ku - kuti iwo adzatero (ndawapanga iwo azilamulira pa zonsezo), kuti iwo aziyang'anira pa zonsezo ndi kumawona kuti izo zonse ziri bwino, kuti chiri chonse chizibala apo za mtundu wake. Tsopano iye ali nazo mphamvu zochitira izo." Mulungu ndiye anati, "Chabwino, ngati zonse ziri zabwino chomwecho, ndipo izo sizingakhoze kukhala china chiri chonse, chifukwa ndi chikhumbo Changa Chomwe. Ndi momwe Ine ndikuzifunira izo. Ndipo Ine ndaziyankhula izo mwanjira imeneyo, ndipo Mawu Anga azibweretsa izo basi ndendende momwe Ine ndimafunira izo. Ndipo ndizimenezo. Izo zonse ndi zabwino!" Kotero Baibulo linati, "Mulungu anapuma tsiku lachisanu ndi chiwiri, ku ntchito Zake zonse."

30 Ndipo chirichonse chinali pansi pa ulamuliro, kuti chizibala za mtundu wake.

Tsopano kumbukirani, "kuti zizibala." Pamene Iye Anaika mbewu mu nthaka, mbewu ikhoza kokha kumela ndi mphamvu ya moyo mkati mwakemo, kuti iyisandulize iyo kuchokera ku njere kukhala chomera, kapena chiri chonse chomwe chinali. Mphamvu Yake yosanduliza! Tsopano, Mulungu anayika mbewu mmenemo, ndi zothekera kuti iyo ikanadzakhala ili chomwe Iye anati iyo ikanadzakhala ili. Ndipo bola ngati iyo ikhala ili mu gulu lake lolondola, iyo ikanadzakhala ndendende basi chimene Mulungu anati iyo ikanadzakhala ili. Izo zinkayenera kuti zikhale mwanjira imeneyo, ndipo anaikonza iyo motero, ndipo naipangira modutsa. Kuti, chirichonse chomwe chingakhale mu mpita wake, mu mzere wake wa Mawu, icho chikanadzayenera kuti chidzidzabala ndendende monga Mawu Ake anati chikanadzachita. Icho sichingakhoze kusuntha kuchoka apo. Icho chaongoledwa ndendende molondola basi.

Kotero, ndi chiri chonse chiri mu chidaliro cha mwana Wake Yemwe, kuti izo zikanadzakhala ziri mwanjira imeneyo, ndiye Mulungu anati, "Zonse ziri bwino, kotero ine ndingopuma. Ndipo iliyonse ya mbewu izo ili ndi mphamvu mwa iyo yokha, kuti idzisandulize yokha kukhala mtundu umene ine ndikukhumba kuti iyo ikhale ili. Ndimmene iyo iyenera kukhala, chifukwa ndaipatsa mbewu iliyonse mphamvu yodzisanduliza, kuti idzipange yokha, mwa zothekera zakezo tsopano kuti idzipange mwa yokha ndendende chimene ine ndikufuna kuti iyo ikhale ili."

Mulungu sanayambe wasinthapo. Chimodzimodzi basi lero monga Iye analiri apo! Mulungu watsimikiza kuti achita china chake. Iye achichita icho. Palibe chomwe chiti chimulepheretse Iye. Iye adzachichita icho.

31 Tsopano zonse zitatha kukhala bwino ndi kuikidwa mu dongosolo, Mulungu anamverera motsimikiza tsopano kuti izi zonse zikanadzakhala ziribwino.

Ndiyeno, pamene Iye anatero, ndiye umo munabwera mdani. Ine ndati…. Mulungu anapereka mphamvu yosintha. Ndipo ine ndimutcha munthu uyu, wokhala ndi mphamvu osati - kuti alenge nayo kachiwiri, koma ine ndiri…. Iye anali ndi mphamvu yolumalitsa, osati yosandulizira; koma yolumalitsa. Tsopano, chirichonse cholumala chimatengedwa kuchokera ku chikhalidwe chake chapachiyambi, pali china chake chomwe chalakwika nacho.Zaka zina zapitazo, pa ulonda, ndikudutsa kupyola mu minda ya chimanga, ine ndinkakhoza kuganiza za, apo panali nthambi yomwe inathyoledwa kuchokera pa mtengo, ndipo inali itagwera pa phesi la chimanga. Ndipo phesilo linali likuyesera mwakukhoza kwake kuti lidzuke mowongoka monga ilo linkayenera kukhalira liri, koma ilo linali litalumalitsidwa chifukwa chakuti china chake chinali chitachitika. Ndipo ndodo inali itatsamira pa ilo.

32 Ndiye ife tikupeza zoyanga zakuthengo m'munda. Zomwe, ochuluka a inu amuna pano, ndipo mwinamwake ena a inu akazi…. Ngati inu mumachokera ku Ketucky. Akazi amagwiritsa ntchito khasu kumeneko mofanana monga amuna, amapita kumunda ndi - ndi khasu, ife timalitcha khasu lakale lakhosi lasekwe, ndi kumadula - zoyangazo. Pakuti, ngati iwe ukanati usadulepo zoyangazo, komwe chimanga chinali mu mzere, monga chonchi ndiye choyangacho chimafikira apo, nkuchigwira chimanga icho, ndi kuchizengeza mozungulira pang'onopang'ono, mophweka kwambiri, monyengerera kwambiri, mwakuti inu mungavutike kudziwa kuti chikukulunga. Ndipo potsiriza chimafika polimbana ndi kulimbitsa, ndipo chimachikoka chimanga chimenecho mpaka icho chitalumala. Chimachikokera icho mokanikizira kwa icho

chomwe, kuchikulunga icho kuzungulira pa zingwe zake zomwe; kuchilumalitsa icho kuchokera ku chomwe icho chinali, kukhala china chakenso. Komabe ndi chimanga, koma icho ndi chimanga cholumalitsidwa.

33 Ndipo ife tonse tikadali mu chifanizo cha Mulungu. Koma ena ndi olumala kwambiri, ngati ana a Mulungu, omwe amayenda mosiyana ndi Mawu Ake ndi ku njira yomwe - yomwe Iye anali nayo ndipo anaipereka kwa ife kuti tiziyendamo. Kuyikamo china chake, dziko limatipotokola ife kutichotsa m'njirayo kutikokera ife pafupi ndi ilo, ndi kutalikira ndi kanjira kowongoka, kopapatiza komwe Iye anatibzalamo ife, kuti tikhale ana a amuna ndi a akazi a Mulungu. Tchimo lachita chinthu choipa ichi kwa ana a amuna ndi a akazi a Mulungu.

34 Wolumalitsayo! Ine ndikudziwa izi zikuwoneka kuti ndi zachilendo kuti tiziyankhula izi mwa njira iyi, "ku - kuti awalumalitse," koma ndicho chomwe iye anali; iye anawalumalitsa, kapena anawapotoza. Kupotoza kumatanthauza "kusinthidwa, kupangidwa china chake chosiyana." Ndipo kulumalitsidwa ndi chinthu chomwecho, kuti chabweretsedwa ndi kudzalumalitsidwa ndi "Kupangidwa mwa njira ina." Komabe iyo ikadali mbewu yomweyo, koma iyo ndi yolumala.

Tsopano ife tikupeza kuti wolumalitsa uyu nayenso anali nako kuchuluka komweko kwa nthawi, kuti awalumalitse, monga Mulungu anali nayo kuti asinthe. Tsopano iye anabzala mbewu yake, kapena, sanabzale konse mbewu yake, iye… m'munda wa Edene. Kuyambira nthawi imeneyo, iye wakhala nazo zaka zikwi zisanu ndi chimodzi za kulumalitsa Mbewu ya Mulungu, Mawu a Mulungu; kuti aziwalumalitsa Iwo, kuwapanga Iwo china chake chosiyana; pamene iye… nthawi yoyamba yomwe Hava anamvetsera kwa iye, nadzipezera yekha kaneno kamodzi kokha…

35 Kumbukirani, poyamba Satana anabwereza Lemba lija momveka basi monga likanakhalira, "Mulungu ananena kuti, 'Inu musamadye za mu mtengo uliwonse m'munda wa Edene'?"(Mukuona?) "Inu musamadye za mu mtengo uliwonse?"

Ndipo kumbukirani tsopano, Hava anati, "Inde, ife tikhoza kumadya za mu mtengo uliwonse; kupatula mtengo umene uli pakati pa munda, ife tisamawukhudze nkomwe iwo." Tsopano penyani iye, mu uthenga wake, anapotoza Mawu amenewo pang'ono pokha basi. Ponena kuti…. Hava anati, "Pakuti Mulungu ananena, kuti, ngati ife tichita ichi, tsiku limenelo ife 'tidzafa.'"

Iye anati, "O, ndithudi inu simudzafa ayi." Mwaona, iye anali m - mwamuna, iye anati, "Iwe, iwe uchite izi tsopano. Ndipo, iwe, iwe uli ngati anthu osadziwa. Iwe, kwenikweni, iwe sukudziwa zinthu zonse. Koma ngati iwe uti udye nao kokha izi, ndiye iwe ukhala nazo nzeru, iwe ukhala nacho chidziwitso. Iwe uzidziwa chabwino kwa choipa ndipo ukhala ngati milungu, iwe, ngati iwe uti udye kokha za nzeru iyi yomwe ine ndiri nayo. Ine ndikuidziwa, koma iwe sukuidziwa.

36 Chomwe, nzabwino kukhala nazo nzeru. Koma ngati nzeruzo ziri zosiyana, ngati nzeruzo siziri zolondola zochokera kwa Mulungu, nzeru Zamulungu, ndipo nkukhala nzeru zachibadwa; ine sindikusamala kaya ndi sayansi yochuluka bwanji yomwe ife tiri nayo, ndi zina zotani, kapena maphunziro, ndi za mdierekezi. Ine nditsimikizira izo kwa inu, Ambuye akalola, mu mphindi pang'ono. Ndi za mdierekezi. Chitukuko ndi cha mdierekezi. Ine ndatsiriza kumene kulalikira pa zimenezo.

Chikhalidwe chonse cha mu dziko lapansi, mphamvu zonse za sayansi, ndi chirichonse, ndi za mdierekezi. Ndi uthenga wake womwe iye analalikira, wa chidziwitso, m'munda wa Edene. Ndipo iye watenga chidziwitso chimenecho, chidziwitso chopotozedwa, chosiyana ndi Mawu ndi chifuniro ndi dongosolo la Mulungu. Ndipo tsopano iye wakhala nazo zaka zikwi zisanu ndi chimodzi kuti achite chimodzimodzi basi zomwe Mulungu anachita, kokha mwa njira yopotozedwa, ndipo watenga kuchuluka komweko kwa nthawi kuti abweretsemo Edene wakewake. Tsopano iye ali ndi Edene pano pa dziko lapansi, ndipo iyo ndi yodzadza ndi nzeru, chidziwitso. Umenewo unali uthenga wake pachiyambi, chidziwitso, nzeru, sayansi. Palibe pomwe Mulungu anayamba wapereka zoterozo. Ndipo Ine ndikufuna inu kuti mupenye mukamphindi. Iye anachita izi, ndipo chifukwa iye anali munthu wa nzeru ya m'dziko.

37 Tsopano, ndi zovuta kunena izi. Izo - ndi zovuta kwambiri, chifukwa kuyankhula kwa anthu omwe amamverera mwanjira yomweyo ine ndimachitira, ndi momwe ine ndakhalira ndiriri kwa zaka zambiri. Koma kuchokera pa kutsegula kwa Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri izo, za Angelo aja basi kuseri kwa phiri kutaliko, Ili lasanduka Buku latsopano. Ndi zinthu zomwe zakhala zitabisidwa, izo zikuululidwa monga Mulungu analonjezera mu Chivumbulutso 10, Iye akanati adzachite izo. Ndipo ife ndife anthu amwayi omwe Mulungu wawasankha, a pa dziko lapansi, kuti ife tikhoze kuwona ndi kumamvetsa zinthu izi; zomwe siziri nthano zina, malingaliro achithupi a munthu akuyesera kuzipanga izo. Ndi Mawu a Mulungu akuwonetseredwa, akutsimikiziridwa, kuti Iwo ndi owona. Otsimikiziridwa, osati ndi sayansi; koma ndi Mulungu, kuti Iwo ali olondola.

Mulungu, monga ine ndinanena poyamba mu uthenga, Mulungu samasowa wina wake kuti azitanthauzira Mawu Ake. Iye ndi wodzitanthauzira Iye Yekha. Iye akamanena kuti zidzachitika, ndipo izo zimachitika. Ndizo, Iye -amazitsimikizira izo, izo zimawatanthauzira iwo.

38 Zaka pang'ono zapitazo pamene, ife anthu achiPentekoste, pamene - mipingo ina inkatiuza ife kuti tinali "openga," ife "sitikanakhoza kutero, Mzimu Woyera chinali chinthu chakale." Koma ife tikupeza kuti lonjezo la Mulungu linali la kwa aliyense yemwe akufuna, ndipo tsopano ife tikudziwa mosiyana. Onani, ndipo zimenezo ndi pang'ono ndi pang'ono basi, chinthu ichi chatseguka. Ndipo tsopano Iye analonjeza kuti zinsinsi zomwe zinabisidwa mu mibadwo yonse ya mipingo zidzaululidwa pa nthawi yotsiriza. Ndipo Iye akutilola ife kuti tidziwe tsopano. Ife tiri pa nthawi yotsiriza. Ife tiri pano tsopano.

39 Tsopano, Satana ndi mwini wa chitukuko. Iye ndi mwini wa sayansi. Iye ndi mwini wa maphunziro. Inu mukuti, "Kodi izo nzoona?"Chabwino, tiyeni ife tiwerenge mu Mawu a Mulungu tsopano, Genesis 4, ndipo tiyeni tibwerere m'mbuyo ndipo tingowona kwa kamphindi. Ine ndikudziwa ine ndikhoza, ngati ine nditalikitsa kwambiri, M'bale Carl mwinamwake andiuza ine. [Winawake akuti, "Ziri bwino." - Mkonzi.]

Koma, Genesis mutu wa 4, ndi ndime ya 16, ikupitirira kutiuza apa, pa chiyambi, zomwe Mulungu anachita mwa cholinga, choti ayike themberero pa mwamuna ndi mkazi, ndi zonse zomwe iwo anali oti azichita; ndipo osati themberero pa iwo, koma kuwauza iwo zomwe zikanati zidzachitike, ndi kuitemberera nthaka chifukwa cha Adamu. Ndipo ife tikupeza pano tsopano, kuti Hava anali ndi mapasa. Ndipo mmodzi wa iwo anali wa Satana, ndi mmodzi wa iwo anali wa Mulungu. Tsopano inu mukuti, "O, ayi! Ayi. Tsopano, M'bale Branham!" Mphindi yokha. Mundipezere ine Lemba limodzi, paliponse, lomwe limanena kuti Kaini anali mwana wa Adamu. Ine ndikusonyezani inu mu Lemba pamene Ilo likuti, "Kaini anali wa woipayo," osati Adamu.

40 Tsopano zindikirani pamene iye anaima apa. Ife tiyambire pa mutu wa 4, poyamba.

Ndipo Adamu anamudziwa…mkazi wake; ndipo iye anaima, ndipo anabala Kaini, ndipo anati, ine ndalandira…(.iye anatero tsopano, ine ndalandira) mwana kuchokera kwa Ambuye

Zoona, izo zinayenera kukhala ziri. Ziribe kanthu ngati iye akanakhala wa chiwerewere kapena chiri chonse, iye amayenera kubwera kuchokera kwa Mulungu, mwaona, chifukwa iyo ndi mbewu Yake, ndi lamulo la mbewu Yake, iyo imayenera kuti ibale kaya ndi mbewu yoipitsidwa, mbewu yopotozedwa, kapena chirichonse chomwe iyo ili. Iyo iyenera kuti ibale, chonchobe. Uko ndi kulamulira Kwake.

Ndipo kachiwiri iye anabala m'bale wake Abele.

Popanda kumudziwanso iye. Adamu anamudziwa mkazi wake, ndipo iye anabala Kaini ndipo anabalanso Abele, mapasa. Satana anagona ndi iye m'mawa umenewo, Adamu madzulo awo.

41 Inu mwaona mkangano waukulu mu pepala kuno, ine ndikukhulupirira mu Tucson tsopano, wa mkazi uyo atabala mwana wachikuda ndi mwana wachizungu, pa nthawi yomweyo. Iye anagona ndi mwamuna wake m'mawa umenewo, ndi mwamunayo madzulo awo. Ndipo bamboyo azisamalira, mzunguyo anati iye azisamalira mwana wakeyo, koma bambo wachikudayo ayenera kuti azisamalira wakeyo. Mukuona? Ine ndikuzidziwa zimenezo, mu kukweranitsa kwa galu ndi zina zotero, izo ndithudi zimatero, ngati izo ziri mu ma ora pang'ono pambuyo pake. Izi zikutsimikizira ichi.

42 Tsopano kuti tisonyeze kumene chitukuko chikuchokera, tsopano tiyeni ife tiwerenge Genesis cha apa, mu mutu wa 4 wa Genesis kachiwiri, ndipo tiwone pamene. Ndime ya 16.

Ndipo Kaini anachoka mu Kukhalapo kwa Mulungu, ndipo anakakhala mu dziko la Nodi, kumbali yaku m'mawa kwa Edene.

Ndipo Kaini anamudziwa mkazi wake; ndipo iye anaima, ndipo anabala Enock: ndipo iye anamanga mzinda, ndipo anawutcha dzina la mzindawo, motsatira… mwana wake, Enock

Chitukuko chinayamba. Doctor Scofield, apa mu Baibulo langa la Scofield, ilo likuti, "Chitukuko choyamba." Zindikirani, ndiye iye anabala ana, ndipo iwo anapanga malimba ndi zoyimba. Wotsatirayo anabala ana, ndipo iye anayamba kuchita zinthu zina, zodabwitsa, kumanga mizinda, ndi - ndi kupanga zida za mkuwa, ndi mitundu yonse ya zinthu. Mwaona, ndi zomwe iye anachita, chinakhala chitukuko choyamba, chomwe chinali cha Chikaini. Iye wachita chinthu chomwecho kudutsa mu mibadwo.

43 Tsopano tiyeni tifike apo ndi ndime ya 25, ndipo tiwone chomwe wotsatirayo anali.

Ndipo Adamu anamudziwa mkazi wake kachiwiri, tsopano, ndipo iye anabala mwana, ndipo anamutcha dzina lake Seti: pakuti Mulungu, anati iye, wandisankhira ine mbewu ina m'malo mwa Abele yemwe Kaini anamupha.

(Ndipo Seti)…. Ndipo kwa Seti, kwa iye aponso kunabadwa mwana; ndipo iye anamutcha dzina lake Enosi: ndiyeno anayamba anthu kuitanira pa dzina la Ambuye.

(Kuchokera ku mbali ya Seti, osati mbali ya Achikaini) Mwaona, aluntha aakulu awo omwe ife tonse timagwirirako kwambiri! Kodi chikominisi lero ndi chiani, kodi mulungu wawo ndi chiani? Ndi luntha, sayansi. Kodi ife tikuchita chiani, mulimonse? Kodi ife tikukhala kuti? Talingalirani mawu awa lero.

44 Tsopano iye alinawo mtundu wake wa Edene, Satana ali tsopano. Mu zaka zikwi zisanu ndi chimodzi izi, iye wapanga (osati kulenga), koma, walilumalitsa dziko lonse la Mulungu; zolengedwa zake, zinyama, kuzikweranitsa, kuzisakaniza; mitengo, zomera, anthu; ngakhale mpaka ku chipembedzo, Baibulo, mpingo; mpaka iye wadzipezera yekha munda wathunthu wa Edene, wa sayansi, chirichonse chikuyenda mwa sayansi. Magalimoto athu, chirichonse chomwe ife tiri nacho, chinaperekedwa kwa ife ndi sayansi, zomwe munthu wachita. Ndipo iye ali naye Edene. Edene wake wamkulu kuno;

Kuti atsimikizire kuti Uthenga uli mu nthawi yake, kuti atsimikizire kuti si m'badwo winawake koma Chivumbulutso 10! Tayang'anani pa kubalitsa mosakaniza lero, kuti apange chabwinoko, kapena, chokongolerako, osati chabwinoko. Tayang'anani pa ana aang'ono lero.

45 Ine ndinali naye mwana wanga wamkazi kwa dotolo wa zamano, dzulo, ndipo iye anati dzino lake linali kugwedera. M'bale uko mu Tuckson, M'bale Norman, anali ndi mwana wake wamkazi wam'ng'ono, ndipo dzino lake linali kugwelukapo. Ndipo wa zamano ananena kuti posachedwapa, iye akukhulupirira, kuti mwina mwake mu nthawi zikudzazi, kuti anthu azidzabadwa, ali ndi mano akumera mulimonse. Ndi chakudya chimene ife tikudya, chakudya cha haibridi. Kodi inu munawerenga mu Reader's Digest, mwezi watha, za Billy Graham, mlaliki wolemekezeka? Kodi inu mwakhala mukumvetsera kwa iye? Ine ndikumupempherera iye tsopano kuposa kale lonse. Pamene iye ankayankhula ndi otembenuza makolala aja, ndi zina zotero, usiku wina, akuziyika izo kwa mlaliki uja. Chinachake chachitika kwa iye. Limodzi la masiku awa, ine ndikuyembekeza kuti iye awona malo ake kumene iye ali, zindikirani, tsopano akuitana kuchokera ku Sodomu, mzinda wopotozedwa uja. Ndipo tsopano zindikirani izi mu Reader's Digest Billy anafooka kwambiri mwakuti iye sakanakhala ngakhale kuchititsa misonkhano yake. Ndipo iwo anamuuza iye kuti azichita zothamanga, azipanga zolimbikitsa thupi, ndi zina zotero. Kotero iye amathamanga mailo tsiku lirilonse, ine ndikukhulupirira izo ziri, kapena china chake, kuti azilimbikitsa thupi.

46 Munthu wavunda. Mtundu wonse wa anthu waonongeka. Chirichonse chiri monga zinaliri mu nthawi ya chigumula. Izo zasokonezedwa kwathunthu, zatembenuzidwira kwina, zasiyana ndi mzere woongoka umene Mulungu anazibzalamo izo. Tchimo, kupyolera mu sayansi ndi chinyengo, zapinda mtundu wonse wa anthu.

Kodi inu munawerenganso pansi pakepo pa nkhani imeneyo, pamene izo zinati, "Mu masiku ano, kuti atsikana aang'ono ndi anyamata akumakhala mu usinkhu wawo wapakati, malingana ndi mamangidwe a thupi, pakati pa usinkhu wawo wapakati, pa usinkhu wa zaka makumi awiri ndi makumi awiri ndi zisanu." Taganizani za izo. Mu kuzindikira za mumtima usiku wina, ine ndinamupeza mtsikana wausinkhu wa zaka makumi awiri ndi ziwiri, mu kusintha kwa thupi, ndinamuitana iye. Ndipo ndizo zomwe dokotala wake anali atamuuza iye. Mwaona ndi mtundu wakugwa, wotsika womka ku gehena wachivundi. Ine ndikudziwa kuti izo sizikumveka mwachikhalidwe, koma ndi mwa Baibulo, onani, kuti izo ndi zoona; ndipo mtundu uno umene ife tiri kukhalamo, kam'badwo kano ka anthu.

47 Tsopano zindikirani lero, kuzipanga haibridi ng'ombe, kuzipanga haibridi mbewu; ndipo sayansi ikubwera mozungulira apo, sayansi yomweyo yomwe ikuchita zimenezo, ikuti, "Izo ndi zomwe zikuwononga mtundu wonse wa anthu." Inu mumawerenga izo mofanana ndi momwe ine ndimachitira. Chabwino, nanga bwanji iwo sakudziletsa izo? Nchifukwa chakuti iwo sangakhoze kudziletsa izo. Mawu a Mulungu anena kuti izo zikanadzakhala mwanjira imeneyo. Koma ngati iwo akanaganiza kwa kamphindi, iwo ali zida zake, monga Yudasi Iskarioti, akuzikhazikitsa ndendende chinthu chimene Mulungu anati chikanadzachitika. Icho chikuchita izo ndendende basi pa maziko awo omwe a sayansi.

Kafukufuku wake wa sayansi, mu kachitidwe komweko komwe iye anamunyengera nako Hava, iye aponso waunyenga mpingo, womwe apo Hava anali choimira. Tsopano, tsopano Adamu choimira apo kachiwiri, kapena Hava, kani, cha mpingo, zindikirani chimene izo zinachita. Kupyolera mu kuyendayenda akufuna chidziwitso, iye akuzemba nadutsa mnzere wa pakati pa chokhoza ndi cholakwika, pa kumvetsera kupotoza kwa Satana, kapena kulumalitsa, kwa Mawu apachiyambi a Mulungu.

48 Ndipo tsopano mipingo lero yakhala yolumala. Tsopano ine sindikuyankhula za anthu, anthu pawokha. Ine ndikuyankhula za dziko la mpingo. Umodzi wapotozedwera njira ina, ndi wina wapotozedwera kwina, ndipo, mwa sayansi. Kachitidwe komweko komwe iye anachitira. Iye wachita kuwopsyeza kwake, Satana watero, kwa pa Yesaya14:12.

Tiyeni tingowerenga izo kwa kamphindi. Mu Buku la Yesaya, tiyeni tiyambire pa mutu wa 14, ndime ya 12.

Wagwa motani iwe kuchokera kumwamba, O Lucifara, mwana wa m'mawa! Wagwetsedwa motani pansi iwe, amene unkawalefula mafuko!

Uyu ndi Yesaya akumuwona iye mu masomphenya, mwaona, mu m'badwo wakudza.

Pakuti iwe unati mu mtima mwako, ine ndikwera m'mwamba, ine ndikweza mpando wanga wachifumu pamwamba pa nyenyezi za Mulungu: ine ndikukhalanso pa Phiri la osonkhana,… mbali za ku mpoto:

49 Cholinga cha Satana, kuchokera ku Edene, chinali choti adzipangire yekha Edene; ndi kudzikweza yekha pamwamba, kotero kuti nyenyezi za Mulungu zikanati zidzimupembedza iye, ana akanati azimupembedza iye. Ndipo iye mwamtheradi wazichita izo tsopano, ndipo pamene iye wachita izi ndi kuzibweretsa izo mu mpingo. Zomwe, ine sindipita mwatsatanetsatane. Aliyense wa inu mumamvetsera ku matepi amenewo mukudziwa za izo. Kuti, ndilo ndendende ora lomwe ife tiri kukhalamo, ndipo ndi Satana yemwe wachititsa izo kupyolera mu ndondomeko ya maphunziro, zokwanira bwino, zabwinoko izi, zabwinoko izo. Ndipo osadziwa nthawizonse, iwo akuyenda kumene molunjika waku imfa. Achititsidwa khungu, akutsogolera akhungu, atsogoleri akhungu a mafuko, atsogoleri akhungu a sayansi, atsogoleri akhungu a mpingo, akhungu akutsogolera akhungu. Yesu anati, "Asiyeni iwo okha, iwo onse akagwera mu dzenje."

50 Apa tazindikira choimira cha ma Edene awiri oyimiridwa moyandikana kwambiri, mpaka pafupifupi kunyenga osankhidwa omwe. Mateyu 24:24 ananena kuti izo zikanadzakhala mwanjira imeneyo. Koma ine ndikufuna ife kuti tiime kwa mphindi pang'ono ndipo tilingalire ma Edene awiri awa, ndipo chinthu chimodzi makamaka, momwe Baibulo limatiuzira ife kuti Mawu a Mulungu anabala Edene uja, ndi momwe Mawu a Mulungu amatichenjezera ife kuti Edene winayo akanadzabwera.Tsopano, ife tikudziwanso kuti payenera kukhala pali Edene wina.

Ngati ife tingati timvetserenso kwa mneneri, Paulo, mu Atesalonika Wachiwiri mutu wa 2. Ine ndikhoza kuwerenga Iwo ngati inu mukufuna kutero.

Iye yemwe akudzikweza yekha; tsiku limenelo silidzabwera, la Ambuye, mpaka munthu wa tchimo uyo akhale ataululidwa,…

… iye yemwe amakhala mu kachisi wa Mulungu, nkumadzikweza yekha pamwamba pa zonse zomwe zimatchedwa Mulungu, kotero kuti iye ngati Mulungu akumapembedzedwa ngati Mulungu.

Taganizani za zimenezo! Tsopano Yesaya 14, mneneri ananena kuti iye anamuwona "Lucifara, mu mtima mwake," kupyolera mmasomphenya pansi pa kudzodza kwa Mulungu, "akunena kuti iye akanadzachita izo." Mu Yesaya, zaka mazana asanu ndi atatu asanafike Paulo, kapena pafupifupi zimenezo. Tsopano apa, zaka mazana asanu ndi atatu zitapita, Paulo akumuwona iye, akubwera ku udindo wake. Zindikirani, izo zikuyambitsa, Edene wake; Edene wake wa mwasayansi, ndi dziko lake la mwasayansi, ndi mpingo wa mkwatibwi wa mwasayansi, zonse pansi pa - mawu a "chidziwitso," maseminare a akulu, madigirii a akulu, madongosolo a maphunziro.

51 Mvetserani, m'bale, mlongo, aliyense wa ife adzayenda mu njira iyo yomwe Florence wayendamo. Ine ndikukupemphani inu, mu Dzina la Yesu, kuti mulingalire Izi. Osati mundilingalire ine. Ine ndi m'bale wanu. Izo, izo si ndizo. Muwalingalire Mawu omwe ine ndikulankhula, a Baibulo la Mulungu. Ndipo muyang'ane mokwanira, zotsimikiziridwa mwangwiro mu Mawu Ake a Mulungu, mu m'badwo womwe tiri kukhalamowu, pomwe ife tiri.Madongosolo awa ali mwamtheradi otsutsa Khristu, mwa iwo eni.

Tsopano, iye ayenera kuti akhale naye Edene, iye anati iye akanadzachita zimenezo. Pano pali Mawu a Mulungu ophweka akunena kuti iye akanadzachita zimenezo, ndipo pano ife tikuyang'ana kumene pa iwo ndipo tikumuwona iye akuzichita izo. Iye wazichita izo ndi mkwatibwi wake wa mwachipembedzo, wa luntha wa mwasayansi. Iye atenga ulamuliro, limodzi la masiku awa, mu Bungwe la Mipingo ya M'dziko lomwe liti lidzakhazikitsidwe. Onse adzakhala ali naye. Kuyesera…

52 anthuwo.. osati chifukwa iwo ndi anthu oyipa. Iwo anabzalidwa mu mzere woongoka uwo, monga chimanga, koma Satana anafetsa zoyanga, zotchedwa sayansi, kafukufuku, maphunziro, madigirii a udotolo. Nthawizina iwo sangakulole nkomwe iwe pa guwa kupatula ngati iwe utawonetsa digirii ya udotolo yochokera ku seminare ina kwina kwake. Zonsezo ndi zolakwika! Osati anthuwo; ndi dongosolo lomwe liri lolakwika.

Ndipo tsopano zachita chiani? Izo zonse zatsogolera apo kachiwiri, ndipo zabweretsa dziko lonse lamphumphu (kupyolera mu gulu la haibridi, kupotoza kwa Mbewu ya pachiyambi ya Mulungu) ku chisokonezo china cha mdima. Koma ndine wokondwa kwambiri kuti Mulungu walingaliranso za ife, kuti Iye akukhozabe kumasuntha pa nkhope ya chikhalidwechi. Iye analonjeza kuti Iye akanadzachita izo, ndi kudzaitana kagulu kakang'ono komwe kati kadzakhale mkwatibwi Wake.

53 Zindikirani apa kachiwiri tsopano, momwe mipingo iyi ikuimiridwira mwangwiro, kapena ma Edene awa. Mulungu, kupyolera mu Mbewu ya Mawu Ake! Ndipo pali chinthu chimodzi chokha chomwe chingawafulumizitse Mawu, ndipo chimenecho ndicho Mzimu, pakuti Iwo ndi Wopereka - Moyo kwa Mawu. Ndipo pamene Moyo mu Mawu ukomana ndi Moyo wa Mzimu, Iwo umabala chirichonse chomwe Mbewuyo ili.

Tsopano zindikirani zomwe zinachitika. Mmunda wa Edene munali chuma cha Mulungu cha kusalakwa, ndipo iyo inali imodzi ya - mibadwo. Mbadwo woyamba unali wa kusalakwa, anthu sanali kulidziwa tchimo. Iwo sanali kudziwa chirichonse cha tchimo. Onse Adamu ndi Hava anali maliseche, koma iwo anabisidwa

ku umaliseche wawo, mwa chophimba cha mzimu pa nkhope zawo. Iwo sankadziwa nkomwe kuti iwo anali maliseche, konse, chifukwa iwo anabisidwa. Pakuti, chophimba cha Mulungu mu malingaliro awo omwe. Iwo sankadziwa kuti kolondola ndi kulakwa ndi chani. Ndipo iwo onse ankaima apo amaliseche, zinkasonyeza kuti chidziwitso chinali chisanabwere apabe kwa iwo, mwaona, kuti iwo anali amaliseche. Awiriwo anali amaliseche ndipo sankadziwa izo ayi.

54 Tsopano ngati inu mungatembenuze, ngati inu mukukhumba kutero, kapena kuti muzirembe izo apo, mu Chivumbulutso, mutu wa 3. Mzimu woyera ukuneneratu mu m'badwo wotsiriza uno, ku m'badwo wa mpingo wa Loadikaya wa chiPentekoste mu masiku otsiriza, iye anati:

…. Iwe uli wamaliseche, ndi wa khungu, ndipo sudziwa izo. Apo pali mbewu ya Mulungu, pansi pa kusalakwa, asakudziwa konse kuti iwo anali amaliseche, pansi pa chophimba cha Mzimu Woyera, ukuwaphimba iwo kutchimo.

Ndipo tsopano mu m'badwo wa mpingo wotsiriza, ife tikupeza apa kuti iwo ali amaliseche kachiwiri, ndipo sakudziwa izo. Koma si chophimba cha Mzimu Woyera. Ndi chophimba chomwe Satana anamuveka nacho Hava kumbuyo uko, chophimba chakukhumbira, chophimba chokhumbirira.

Iwo ali onyasa kwambiri mpaka iwo sakudziwa kuti iwo ndi amaliseche, akazi athu pa msewu, atavala akabudula, zovala za mwa chigololo…

55 Winawake anatumizira ine chidutswa cha mu pepala tsiku lina, cha diresi ya tsopano iyi iwo ati adzivala, ine ndikuganiza, mainchesi khumi mdi anayi kuchokera mchiuno, kapena china chake. Ndipo ine ndikudabwa ngati azimayi athuwa akuzindikira kuti icho ndi chophimba cha kukhumbira.

Tsopani inu mungati, "Ine ndikhoza kutsimikizira, pamaso pa Mulungu, kuti ndine osalakwa pa zachigololo zirizonse kwa mwamuna wanga, kape Ine" …. Zonse izi, komabe, pachiweruzo, inu mudzatchedwa "wachigololo." Baibulo linanena chomwecho. Yesu anati, "Yense yemwe ayang'ana pa mkazi namukhumbira iye, wachita chigololo ndi iye mu mtima mwake."

56 "Akhungu, amaliseche, ndipo sakudziwa izo!" osati akazi osauka aang'ono awo kunja uko; palibe kanthu ndilinako kotsutsana ndi iwo. Ndi choipa icho! Ndipo kachitidwe ka mpingo kakuwoneka kuti akulephera kuti kazindikire izi kapena kuima motsutsana nazo; nkumawalola iwo kulidulamo tsitsi lawo kudzipentapenta, ndi zazifupi ndi zinthu, pansi pa dzina la chikhristu. Ndi chinthu choipa bwanji chomwe icho chiri! Mwaona, iwo ali amaliseche kachiwiri, mu Edene wa satana, ndipo sakudziwa izo ayi. Iwo sakudziwa izo.

Ine ndikukhulupirira ine ndikuwona, mwina mwake, kuyang'ana kutsidya linalo, dziwe losambiramo, komwe akazi ali kumeneko tsopano. Ngati mkazi uyo akanazindikira kokha chimene iye akuchita, koma iye sakudziwa icho. Iye ali maliseche. Thupi lake ndi lopatulika. Iye amavula zovala zake zomwe Mulungu anamuveka nazo iye, ndi khungu, chifukwa cha m'badwo uno. Iye mowilikiza akuzidulapo izo. Iye ali maliseche, pansi pa mawu akuti "chitukuko, maphunziro apamwamba, chitukuko chabwinoko, makhalidwe apamwamba."

Mundilole ine nditsimikize kuti izi zikulowa mkati. Zonsezo ndi za mdiererkezi, ndipo zidzawonongedwa pakudza kwa Ambuye Yesu. Izo zidzawonengedwa, chidutswa chirichonse cha izo sipadzakhala chinthu chimodzi chiti chidzatsalire. Ndipo, O, mzanga, kudutsa fukoli, pamene inu mukumvetsera kwa ine muno mu Phoenix, - taganizani za zinthu zimenezo! Inu muli pano mukumvera kwa izo. Tsopano, Yesu ananena kuti, "Izo zikanati zidzanyenge osankhidwa ngati kukanakhala kotheka."

57 Mzimu woyamba unali… chophimba choyamba chinali chophimba choyera, Mzimu Woyera - ndipo iye sankayenera kuti aziyang'ana kunja kwa Icho. Koma pamene - pamene Satana anayamba kuyankhula kwa iye za chidziwitso, iye anangoti asuzumire pang'ono dziko. Ndipo ndizo ndendende zomwe mwana wake wa mkazi, mpingo, wachita. Inu mumayenera kuwona, inu mumayenera kumavala ngati katswiri wina wa pakanema, kapena anyamata amayenera kuti azichita ngati Elvis Presley kapena - kapena Pat Boone, kapena ena a anthu amenewo, pansi pa dzina la chipembedzo. Pat Boone ndi wa Mpingo wa Khristu. Elvis Presley ndi wachiPentekoste. Makhalidwe awiri aziwanda omwe aliponyera dziko muchisokonezo choipa kuposa momwe Yudasi Eskarioti anachitira paku mupererka Yesu Khristu. Iwo sakudziwa izo. Anyamata amenewo sakudziwa zimenezo. Palibe chimene ine ndiri nacho chowatsutsa iwo - anyamata amenewo, amuna, ndi mzimu umene ukuwachititsa izo.

58 Basi mukaponda kumbali iyo pang'ono kamodzi, kuzilola zoyanga izo zingopeza kugwira kumodzi kuzungulira nkhusu ya chimanga icho, nthawi imodzi, muone zimene zitachitike; chimangacho chapita. O, eya, izo zamutenga kale iye. Ndipo umo ndi momwe izo ziti zichitire. Izo zizichita icho nthawi iliyonse. Hava anangotenga kusuzumira kamodzi kokha pa dziko.

Nipo ndiloleni ine ndinene china chake kwa inu, m'bale ndi mlongo. Mu Yohane oyamba, mutu wa 2 ndi ndime ya 15, ife tikhoza kuwerenga izo ngati tifuna kutero, Baibulo limati:

…. Ngati ife tikonda dziko, kapena zinthu za dziko, ndi chifukwa chakuti chikondi cha Mulungu sichiri ngakhale mwa ife.

59 Tsopano, mawu apo si dziko; ndi mawu a Chigriki, ndi Kosmos, chimene chimatanthauza "dongosolo la dziko." Ngati ife tikonda mafashoni a pa dziko lapansi, adzikoli, ngati ife tikonda kachitidwe ka tsikuli, ngati ife tikuganiza "ino ndi nthawi yodabwitsa, o, ife tiri nazo zinthu zonse izi," ngati inu mukuganiza izo, ndi chifukwa chakuti kuganiza kwanu ndi kolakwika. Iko ndi kopotozedwa ndi mdierekezi. "pakuti ngati inu mukonda dongosolo la mdziko, ndi zinthu za m'dziko lino, ndi chifukwa chakuti chikondi cha Mulungu sichiri ngakhale mwa inu." Muzikumbukira zimenezo. O Mulungu! Taonani zomwe ife tikuyang'anapo!

60 Pano ine ndikufuna kuti ndiime mphindi yokha ndi kukuuzani inu kankhani kakang'ono. Ine ndinamumva wopempheretsa ku Nkhondo Yoyamba ya Dziko Lonse. Iwo anali ataponya…Monga Satana pachiyambi, pamene iye anabwera kumunda wa Edene. Iye sankakhoza kudziwononga kudzikumbamo Mbewu zija. Iye sakanakhoza kudziwononga izo. Koma iye anadzipemerera izo ndi chiphe, ndipo icho chinalumalitsa, iyo siyinabereke mwamtundu wake. Iyo inalumalitsa Mbewu ya pachiyambiyo. Ndipo ndi chomwe ali ndondomeko yonse iyi ya chipembedzo. Iwo akadali ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, koma iwo ali mukulumalitsidwa. Iwo amapita ku tchalitchi, amafuna kumachita bwino. Sisitere samalowa nkomwe usisitere kuti akhale mkazi wankhanza. Mtumiki samadutsa nkomwe mu sukulu kungoti akhale - mu - munthu woipa. Inu simumajowina nkomwe tchalitchi, ndi kumagwirana chanza, kuika dzina lanu pa buku, kapena chirichonse chimene inu mumachita mu mpingo wanu, kuti mukhale munthu woipa. Inu mumachita zimenezo kuti mukhale munthu wabwino. Koma ndi chinyengo, ndi kulumala kumene kumachititsa izo. Satana anachipemerera icho. Mwaona?

Mulungu sanayambe wakhala konse ndi bungwe. Palibe chinthu choterocho paliponse chopezeka mu Mawu a Mulungu. Mulungu ndiye bungwe lanthu, ife timakhala bungwe mwa Iye, Thupi, mwa Mulungu, kumwamba. Ndiko kulondola. Maina athu ali pa Buku la Moyo wa Mwanawankhosa. Zindikirani,

61 koma, onani, ine ndikudziwa ndi zolimba kwambiri, koma Ine - ine ndikufuna kuti inu mupirire pang'ono pokha ngati inu mungatero.

Mu nthawi ya nkhondo ya m'dziko lonse…. Mundikhululukire ine chifukwa chochoka ku phunziro langa. Koma kuti tipange fundo iyi, Ine ndikufuna kuti ndikupatseni inu kusanthula kwanga kwa zomwe Satana anachita mu Edene: anapereka mpemera wa chiphe chowopsya. Kodi inu mungakonde kuti mudziwe chomwe chopemerera icho chinali? Ine ndikhoza kukuuzani inu. Ine ndiri nako kapangidwe kake, mawu awiri: kusakhulupirira, zomwe ziri zotsutsana ndi chikhulupiriro, anapemerera kusakhulupirira, kukaikira. Ndipo sayansi inadzaza mu malo ake. Pamene pali mphanga, imene inalowa mu Mbewu, Satana anadzadzitsa mphanga imeneyo ndi chidziwitso ndi sayansi ndi chitukuko, ndipo izo zinalumalitsa, chilengedwe chathunthu chonse cha Mulungu.

62 Ine ndikudziwa kuti inu muganiza kuti ine ndikukutengerani inu pa nthambi, koma ine ndiri pa nthambiyo limodzi ndi inu. Ndipo ife tonse tiri pano kuyesera kuti tipeze zomwe tingakhoze kuzichita. Ife sitikunena zinthu zimenezo kuti tikhale osiyana - ife tiyenera kukhala owona mtima.Ife, aliyense, tidzafika ku mapeto a msewu, pamene ife titi tidzakayankhire pa mawu aliwonse.

Pakali pano, ife tikudziwa kuti maliwu athu…. Pamene ife tibadwa, kulira kwathu koyamba kwakung'ono kumapita pa tepi. Iyo idzaseweredwanso mobwereza paTsiku la chiweruzo. Ngakhale zovala zomwe mukuvala zidzasonyezedwa pamaso panu, pa Tsiku la Chiweruzo. Ngakhale sayansi yazipeza zimenezo, mwa televizioni. Mukuona, televizioni siimapanga chithunzi, iyo imangochidutsitsa icho. Mtundu wa zovala, nthawi iliyonse yomwe inu mumasuntha, maganizo aliwonse ali m'malingaliro mwanu, mwamtheredi amasungidwa pa kaundula wa Mulungu. Ndipo chinthu chachikulu icho chidzaikidwa patsogolo panu pomwe, ya madiresi oipa awo omwe inu mumavala; nthawi iliyonse yomwe inu munkapita kometetsa tsitsi, kukadula tsitsi ilo lomwe Mulungu anakupatsa inu. Izo zidzakhala ziripo. Inu mudzakayankha chifukwa cha izo. Inu simungakhoze kupanga kusuntha pamenepo, palibe ngakhale malingaliro okha a mtima wanu pamene inu mukuzichita izo, adzaseweredwa pamaso panu pomwe. Mudzazithawa bwanji? "Ife tidzathawa bwanji ngati ife tichikana chipulumutso chachikulu choterochi?" mukuwona? Ife sitidzathawa. Kusuntha kulikonse, ndi malingaliro a mu mtima, zimalembedwa kumene mu dera lina, ngakhale mtundu wa zovala zomwe inu mumavala. Televizioni, televizioni yoonetsa mtundu imatsimikizira izo apo pomwe, imazikoka izo ndi kuzisonyeza izo, mwaona, ndipo izo ziri mu dera limodzi lokha kuchokera ku atatu omwe ife tikukhalamowa. Mukuona?

63 Tsopano momwe chiphe chakanthira mpingo, chakanthira dziko lapansi! Chiphe cha Satana pa Mbewu, chaika mphanga mwa iyo ndi kuipangitsa iyo ikhale yolumala. Mochuluka chulukira, iye akumira mozama mu mitima ya mipingo, ndi mu mitima ya anthu ndi chirichonse, sayansi, sayansi. Mpaka awo akhala malo omwe mtundu wa anthu, kukhala obalidwa mosakaniza…. Ine ndikukhulupirira mbewu iliyonse iyenera kumabala za mtundu wake. Ndipo mtundu wa anthu, ndi mbewu, ndi zonse zikubalitsidwa mosakaniza, zatifikitsa, ife pa malo; pa kudya chakudya chathu kuchokera mu nthaka, chomwe, matupi athu, akupangidwa kukhala a haibridi, icho chaika malingaliro athu onse….

Tsopano, ngati matupi athu akugwa, kuyambira pausinkhu wa zaka makumi awiri mpaka makumi awiri ndi zisanu chifukwa cha makhungu owonongeka, mwa zakudya za haibridi, kodi makhungu a ubongo wathu sanaonongeke? Kodi awo si makhunguwo, nawonso? Ndi chifukwa chake Ricky amathamanga kudutsa mu msewu kuno, ndi ndodo yotentha iyi; pamene Ricketta, Elvitta, ndi ambiri a iwo, monga ife tikuwatchula iwo dzina, kunja kuno ovala mwatheka pamaso pa anthu, osokonezeka muubongo, alibenso malingaliro a kuwoneka bwino ndi makhalidwe.

64 Ku nkhani yanga yaying'ono. Wopempheretsa uyu anati iye anali ali uko ku chipatala, ndipo anati anyamata ambiri anali ali mu hema, ena…. Iye anali atangobwera kumene kuchokera kunja. Iye anati iye anapita kumeneko ndipo bwana wina anamuuza iye, anati, "Opempheretsa, ife tikufuna kuti tiyende kupita kunja, kuti tikaiwone minda kunja uko." Uko anali ataponyerako mpweya wa mpiru ndi kulolini, monga iwo ankachitira m'masiku amenewo.

Ndipo anati, "Ine ndinakafika uko, M'bale Branham," anati, "uko kunalibe khungwa pa mtengo, uko kunalibe kuphukira kwa udzu. Uwo unali mmawa wa Chiukitsiro." Iye anati, "Uko kunali mathanki owonongeka akale kumusi uko, bwanayo amayenera kukapeza chiwerengero cha iwo, ndi kukawona ngati kunali chirichonse chomwe chikanakhoza kuchitidwa kwa iwo, pafupi ndi Argonne Forest yayikulu." Anati, "Pamene ine ndinali nditaima apo mwa ndekha," anati, "Ine ndinayang'ana mmwamba, ndinati, 'O Mulungu, uku ndi komwe izi zonse zikudzafikako.'"

Ndithudi, zonse izo zikubwera. Izo zonse zitawotchedwa, popanda moyo paliponse konse, udzu utawotchedwa; mtengo, ndi mipweya imeneyo, mitengo itaphedwa, chirichonse chinali chitaphedwa, chitapindika, chikulendewera pansi, pamene zipolopolo ndi zinthu zinazing'amba izo.

65 Ngati icho sichiri chithunzi cha dziko lero, pamene Satana akupemerera kusakhulupirira kwake, kupanga haibridi kwake, sayansi yake, chidziwitso chake! Mpaka, chimene icho chinali pachiyambi, pamene Mulungu anamuika Adamu ndi Hava m'munda, paradiso wokongola uja wopanda imfa, wopanda matenda, wopanda chisoni, ndipo chiri chonse chiri changwiro mu dongosolo, taonani zomwe DDT wa Satana wachta! Ilo liri mu chisokonezo. Palibe kanthu komwe katsalira mwa ilo.

Iye anati, "Iye ndinayamba kulira. Ine ndinayenda chobwerera, ine ndinakopedwera ku thanthwe." Anati, "Ine ndinangopita apo ndi kukayang'ana pa mwalawo, ndinaugubuduza iwo. Pansi pake pa mwalawo panali duwa liling'ono loyera likumera, chinthu chokha cha moyo chomwe chinatsalira, chifukwa ilo linali litabisidwa ndi thanthwe."

Mulungu, Thanthwe langa, tibiseni ife lero, O Mulungu, pamene ziphe izi zikuwukira paliponse mu dzina la sayansi ndi maphuziro. Tibiseni ife. Ndisungeni ine mpaka tsiku limenelo, O Mulungu, ndilo pemphero langa. [Winawake pa nsanja akuti, "Musaike malire a nthawi aliwonse, M'bale Branham." - Mkonzi.] Tsopano ine ndikuyembekeza kuti ife, aliyense, tiri pansi pa Thanthwe limenelo, Khristu.

66 Ine ndinali nditalalikira basi tsiku lina, ambiri a inu munazimva izo. Ine ndinali kupita uko ndikudutsa mu nkhalango, ndikusaka, ndipo ine ndinakopedwa kuti nditembenuke. Ndipo ine ndinayang'ana, ndipo apo panali katoni yopanda kanthu ya ndudu kapena paketi, kapena chimene inu mumachitcha icho. Ndipo ndi kampani, ine sindikumverera kuti nditchule dzina lawo, koma kampani ya fodyayo inali, iwo ali ndi chodzinenera, "Sefa ya Mwamuna Woganiza, Kukomedwa kwa Mwamuna Wosuta."

Ine ndinayamba kuyendabe chotsika - mopitirira pang'ono mnkhalango, ndipo Chinachake chinandikopa ine, "Bwerera ku paketi ya ndudu ija."

Ine ndinaganiza, "Atate Akumwamba, ine ndikupita kumusi uku ku mtengo uja kumene agologolo aja anayankhulidwa nakhalapo ndi Inu, m'mawa wina. Nchifukwa chiani Inu mukundiitanira ine kuti ndibwerere?"

Ndipo Chinachake chinati, "Uli ndi ulaliki ukubwera wa Lamlungu. Nkhani yako yalembedwa pa icho." Ine ndinaganiza, "Pa paketi ya ndudu?" Ine ndinabwerera. Ndipo ine ndiyamba kuganiza, "Sefa ya mwamuna woganiza,"…….ndi chinyengo bwanji chomwe icho chiri! Ngati munthu akanakhala munthu woganiza, iye sibwezi akusuta konse. Koma, inu mukuona, anthu amameza zimenezo.

67 Ine ndikukhulupirira zinali zaka ziwiri zapitazo, pamene ine ndinali mu umodzi wa misonkhano yaikulu, ine ndinapita ku chiwonetsero cha m'dziko pamene icho chinali ku Gombe la kumadzulo. Ndipo iwo anali ndi chithunzi cha Yul Brynner ndi ambiri a iwo uko. Ndipo asayansi, ambiri a iwo, anali mu holo yomweyo, za kuwopsya kwa kusuta. Momwe iwo amakokera utsi uwo kudutsa pa nsangalabwi, ndipo ankatenga Kangowi kakang'ono ndi kuchotsapo chikonga pamenepo ndi kuchiyika icho pa nsana wa khoswe, ndi kukamuika iye mu khola, mu masiku asanu ndi awiri iye anali atadzaza ndi khansara iye sankakhoza ngakhale kuyenda. Mukuona? Iye anati…. Anamukoka iye kudzera m'madzi.

Anati, "Sefa!"

Anati, "Sefa? Palibe chinthu choterocho." Anati, "Inu …." [Tsopano, iyi ndi sayansi iyo yeni]…. Iwo

anati, "Inu simungakhoze kukhala ndi utsi kupatula ngati inu muli ndi phula. Phula limapangitsa utsi."

68 Ndipo chinthu chokha chomwe chiri, ndi njomba, kuti azigulitsa ndudu zochuluka pachimenecho. (ngati, ine sindikuyembekezera mukuganiza kuti ndine wosinjirira kapena wotengeka) . Mdierekezi uyo mwa munthu, ndi yemwe amamupangitsa iye kusuta, kuti adziphe yekha. Pamene Iye - iye amafuna chikonga cha ndudu imodzi, chomwe chingapereke kukhumba kwake, tsopano kampani imabwera mozungulira ndi njomba yonyenga, nkuti, "Sefa ya munthu woganiza." Iye amayenera kuti adzisuta ndudu zinai kapena zisanu, kuti apange phula lochuluka mwa iye (kuti zimukhutitse iye) momwe inu munkachitira ndi imodzi. Achimereka kugulitsa imfa kwa abale awo ndi alongo! Ine sindikuzimvetsa izo.

69 Komabe mmenemo, ine ndinaganiza, "Ilipo Sefa ya munthu woganiza izo ndi zoona."

Tsopano ngati munthu akusuta, kumbukirani, izo zimapereka kukoma kwa munthu wosuta. Ndiye, ngati inu simungakhoze kukhala ndi …. Kukhutitsa chikhumbo cha kusuta mpaka inu mutapeza utsi mmenemo ndi kupeza…. Ziyenera kupereka kukomako. Kotero iwe umasuta ndudu zinai, kapena zisanu, ndi kulipira zambiri pofuna iko kuposa momwe iwe ukanachitira ngati iwe ukanangosuta ndudu imodzi yachizolowezi. Mwaona, ndi njomba, njomba ya malonda; kuwanyenga anthu, Achimereka.

Pamene ine ndikamaganiza za Valley Forge, George Washington; ndi magawo awiri pa atatu a asirikali ake, ndipo osavala nsapato pa mapazi awo, pa tsiku lozizira lija, kuti atipangire ife chuma chomwe ife tirimo! Ndiyeno Achimereka akumamugulitsa Mmereka, m'bale wake ndi mlongo, imfa, pansi pa njomba yabodza, chifukwa cha phindu lauve, muzu wa choipa chonse. Chibaba cha ndalama, chikondi. Chinthu chonsecho chachita misala, sakudziwa kuti chinthu chonse ichi chidzaonongeka!

Koma ngati inu simupeza utsi uliwonse, inu simingakhoze kukhala ndi kukomako. Ndiye ine ndi maganiza, "Ilipo Sefa ya munthu woganiza." Sefa ya munthu woganiza! Ndipo ine ndinaikapo nkhani yanga kuchokera pa "Sefa ya munthu woganiza imapereka kukoma kwa munthu woyera."

70 Kotero ine ndinaganiza kuti zipembedzo zathu zachita zochuluka kwambiri monga izo, kuwatengera anthu mkati ndi kumadzitcha okha AKhristu omwe ali achisawawa. Chiani? Iwo amakhala nawo ochuluka mu chipembedzo chawo kapena mmabungwe. Ife timakhala nawo ambiri mmenemo chifukwa ife timawalola iwo kuti azibweramo pansi pa ichi, icho, ndi chinacho, ndi chirichonse. "Izo sizimapanga kusiyana kulikonse, bola ngati iwo ayika dzina lawo pa buku ndi kumati iwo ndi MKhristu. Ndizo zonse. O, 'mwa chikhulupiriro inu munapulumutsidwa.' Inu mumayenera kukhulupirira." Mdierekezi amachita chinthu chomwecho. Inu muyenera kuti muzibadwa kachiwiri, ndipo izo zimabwera kupyolera mu Sefa ya Mulungu.

Tsopano ilipo sefa ya munthu woganiza. Ine ndaigwirizira Iyo mu dzanja langa. Iyo siingapereke kukoma kwa chipembedzo, koma Iyo ndithudi idzakwaniritsa kukoma kwa munthu woyera, inu mukudziwa.

71 Mkazi wa tsitsi lodulidwa angakhoze bwanji kubwera konse kudutsa mu Sefa imeneyo? Angakhoze bwanji mkazi wovala akabudula kubwera nadutsa mwa Iyo, kapena mathalauza, pamene Baibulo limati, "Ndi chonyasa kwa Mulungu, kuti mkazi avale zovala zomwe ziri zoyenera kwa mwamuna"? Ndipo angakhoze bwanji mwamuna yemwe amaganiza chirichonse za iyemwini, kubwera kuno ndi kuvala ngati akazi, kumalola tsitsi lake lizikula ngati mkazi, kutsikira mmaso mwake, ali ndi mangongo, ndipo litapiringizidwa monga choncho? Iye akumavala zovala zamkati za mkazi wake. Mkaziyo akuvala zovala zake zakunja. Sefa ya munthu woganiza? Mwamuna woganiza sangachite zimenezo, kapena mkazi woganiza sangachite izo. Mawu a Mulungu sangazilole izo kuti zidutsiremo. Palibe kanthu kamodzi kangakhoze kudutsa mu Mawu amenewo. Iwo ndi Mzimu Woyera, ndipo Iwo umawabweretsa Mawu mkati mwanu, ndipo Iwo umapereka kukoma kwa munthu woyera.

72 Taonani lero, Ricketta pa msewu, wokondedwa, mapangidwe okongola omwe Mulungu anapereka kwa iye, ndipo Satana akugwiritsa ntchito iwo. Ndipo iye amadziveka yense mopanda khalidwe kwambiri, osadziwa kuti sabata kuchokera lero iye akhoza kukhala akuvunda m'manda. Ndikubwera pansi mu msewu kuno si kale litali. Ine ndinali ndikulalikira mu msonkhano waukulu ku Assemblies of God uko ku Gombe la Kumadzulo, mu msonkhano uko ku Southwestern Bible School. Dona wamng'ono akuyenda chotsika ndi msewu, wamng'ono… atavala zovala zazing'ono izo, (bikini, chirichonse chimene inu mumazitcha izo,) zilesi zikulendewera apo, atavala chipewa cha wolishya ng'ombe (cowboy) ndi nsapato.

Ine ndinali kupita chokwera ndi msewu. Ine ndinaganiza, "Kamunthu kakang'ono kosauka, mwana wa amayi ndi adadi ena, anaikidwa kuno kuti adzakhale mwana wa mkazi wa Mulungu, ndipo wakhala nyambo ya nsampha wa mdierekezi." Ine ndinaganiza, "Ine ndikukhulupirira ine ndingotembenuka ndi kubwerera, ndi kukamuuza mwana uyo." Iye ankawoneka kuti anali wa pafupi usinkhu wa Sarah wangayo apo, zaka khumi ndi zisanu ndi ziwiri, usinkhu wa zaka khumi ndi zisanu ndi chimodzi, kapena chinachake. Ine ndinaganiza, "Ayi, ine kulibwino ndisatero. Ine ndingopitirira pa mseuwu ndi kukamupempherera iye. Ngati winawake andiwona ine nditaima ndi kuyankhula kwa iye…. ine kulibwino ndisachite izo."

73 Tsopano, ndipo mvetserani, ana a Mulungu, inu mukufika mu malo omwewo, a Yezebeli awa a tsikuli

amasewerera kwa inu, koma mwamuna woganiza amaganiza poyamba. Iye akhoza kukhala wokongola kwambiri, izo zikhoza kukhala kuti "Ine ndikhoza kukomana naye iye," koma izo zikugulitsira iwe moyo wako, mnyamata; ena a atsikana inu, kwa ma Ricky awa! Sefa ya mwamuna woganiza imapereka kukoma kwa mwamuna woyera.

Inu bambo wokwatira, pamene inu muwawona akazi awo pa msewu monga chonchi, inu ana a Mulungu, kodi inu simukuzindikira zomwe zinachitika pa chiyambi kumayambiriro? Pamene sayansi inali itawapanga akazi kukongola kwambiri mu dziko la chigumula, mpaka ana a Mulungu anadzitengera ana aakazi a anthu (osati ana aakazia Mulungu), ndipo Mulungu sanaziiwale konse izo. Iwo anachiwononga chinthu chonsecho; sayansi, kukongola. Izo zikanakhala chomwecho…. Inu mukuzindikira kukongola kwa akazi kukukwera mu masiku otsirizawa, ndi chizindikiro cha mapeto; Mulungu wazitsimikizira izo. Kotero, muzigwiritsa ntchito Sefa ya mwamuna woganiza, inu mudzakhala ndi kukoma kwa mwamuna woyera. Izo zidzakugulitsirani inu banja lanu. Izo zidakugulitsirani inu udindo wanu. Izo zidzakugulitsirani inu chirichonse chomwe inu muli nacho; pambali pa icho, solo yanu! Izo zidzaliswa banja lanu. Izo zidzapangitsa mwamuna wina kudzawalera ana anu, kapena mkazi wina kuwalera ana anu.

74 Tengani Sefa ya mwamuna woganiza, iyo idzapereka kukoma kwa mkazi woyera. Pamene inu muwuyamba wa kunyumba ya ometa, kapena chinachake chimzake, ndipo iwo nkukuzani inu, "Inu mudzikhala ndi kupweteka kwa mutu, inu mukudziwa." Tengani Sefa ya mkazi woganiza, chimene Baibulo linanena, onani, ndiye tembenukani ndi kuchokako uko. Mukuona? Inu musachite zimenezo. Ine ndi m'bale wanu, ndipo ndimakukondani inu. Palibe chomwe ine ndiri nacho mokutsutsani inu. Mulungu akudziwa. Ndipo ndi chimene chimandipangitsa ine kunena zinthu momwe ine ndimachitira, ndi chifukwa cha - cha chikondi cha Mulungu kwa inu. Ngati mwamuna angapite kunja uko ndipo iwo nkusakuuzani inu, abusa anu kumakulolani inu kukhazikika ndi kumachita monga choncho, iye sakukondani inu. Iye sangakhoze kumakukondani inu. Ine sindikanafuna chikondi cha mtundu umenewo pa akazi. Ine ndikufuna ndizikhala ndi kukoma koyera pa mlongo wanga. Ine ndikufuna iye akhale kwenikweni mlongo wanga. Osati winawake wokhoza kunena, winawake wonena za iye kukhala wokongola kwambiri, ndi mmene aliri, ndi ngenge zachogololo zokongola izo, "Iye amapita ku wanga…." Ha - nha. Ayi. Ine ndikufuna iye akhale dona!

O Ambuye, ndisungeni ine pansi pa Thanthwe. Inde. Mu Aefeso 5:26, njira imodzi yokhayo yomwe inu mungakhoze kudzera mu Thanthwe limenelo, ndiko, "Kutsukidwa ndi madzi olekanitsa mwa Mawu." Ndiko kulondola.

75 Tsopano, musamulole mdierekezi uyu apemerere pa inu maphunziro ake. Ayi, ayi. Izo zidzapha chikoka cha inu. Musamulole mdierekezi kuti atenge zakuti, "Chabwino, ndine wa mp ingo umene amayi anga ankapitako, kumene bambo anga, agogo anga aakazi." Musamulole mdierekezi apemerere pa inu zimenezo. Baibulo linanena kale, pa Mibadwo ya Mpingo Isanu ndi iwiri, ndi zinthu pamenepo, izo zonse zapita mpaka ku mbewu! Ndiko kulondola. Chinthu chonsecho chavunda. Chinthu chonsecho ndi bala lonunkha. Musamulole iye apemerere pa inu, kuti, "Chabwino, ndi maganizo apamwamba. Ife ndife ophunzira kwambiri kuposa momwe tinaliri mu masiku akale." Musamulole mdierekezi ayike izo pa inu.

Ine ndakusonyezani inu purogramu yake yonse ya chitukuko, maphunziro ndi sayansi. Iye wazifikitsa izo mpaka mu mpingo momwe, ndipo musamvetsere kwa izo. Muchotse mutu wanu kwa matelevizioni onyasa akale awo ndi zinthuzo!

76 Ndipo nkhani yathu ikuti "musakhale otengera, koma inu mukhale osandulizidwa." Osati kulowamo ndi kumati, "ine ndinatsimikiziridwa, Lamlungu." Ayi. Pitani umo ndi kukasandulizidwa pakali pano, kusandulizidwa kuchokera ko chomwe inu muli, kupita ku chimene Mulungu akufuna kuti mukhale.

Tsopano, izo zimatengera pa mtundu wa mbewu imene ili mwa inu. Ngati ili mwa inu. Ngati iri mbewu yaluntha, ya za maphunziro yomwe yaikidwa mwa inu, pali chinthu chimodzi chokha chomwe iyo ingakhoze kuchichita, kukulumalitsani inu, basitu, kwa mwana wamwamuna kapena mwana wamkazi wa Mulungu. Ndicho chinthu chokha iyo ingakhoze kuchichita.

Anthu lero, pamene ine ndikuyang'ana kunja, iwo akumachita ngati kuti iwo samakhulupirira nkomwe kuti kuli Mulungu.

77 Mundikhululukire ine kufotokoza uko. Ngati kumverera kwa winawake kukupwetekedwa ndi izi, ine sindikutanthauza kutero. Ma Lamlungu angapo apitawo ine ndinaitanidwa, ndi mwana wanga yemwe wa mkazi, kuti ndi bwere pa televizioni kuti ndidzawonere kuimba kwa chipembedzo. Izo zimakhalapo Lamlungu mmawa. Ine ndinkafuna kuti ndimumve Oral Roberts pa purogramu yake, ine ndinawauza iwo kuti andiuze ine. Anati, "Inu muimve iyi, ndi nyimbo yopambana ikuimbidwa." Mwana wanga wamwamuna ataima apo, anandiuza ine za iyo, nayenso.

Ndipo ine ndinayatsa chinthu chimenecho….Ife timachita kubwereka kwa mkazi yemwe ali ndi televizioni mu nyumba yake. Ine sindimalingalira konse kuti ndidzakhale nayo mu nyumba yanga. Ayi, bwana. Ine sindimachifuna chinthu chimenecho mu nyumba yanga. Ine ndingachiwombere icho ndi mfuti

yanga. Ine sindimafuna chirichonse chochita ndi chinthu choipa icho. Ayi, bwana! Koma, anatenga…..

78 Mundilole ine ndikuuzeni inu za aku Arizona inu pano. Inu mumawona kusanthula kuja tsiku lina, kwa masukulu, sichincho inu? Magawo makumi asanu ndi atatu pa zana a ana mu masukulu aku Arizona akuvutika ndi kuperewera kwa maganizo, magawo makumi asanu ndi limodzi ndi zisanu ndi ziwiri pa zana a iwo anali chifukwa choyang'ana televizioni. Nanga bwanji zimenezo? Inu kulibwino muzigwiritsa ntchito mfuti yanu! Mwaona? Tsopano, musamulole mdierekezi apemerere pa inu ndi zimenezo. Ayi, bwana.

Tsopano anthu, monga ine ndinanena, anthu amachitangati iwo sadzasowa kuti adzabwere ku Chiweruzo. Anyamata awa ndi asungwana, iwo anali ndi banja lina la Chimwenye, ndi gulu lonse la zinthu. Ine ndikuganiza munthu wotchedwa Bambo Pool ndiye mkulu wa izo. Ndipo ngati ine ndinayamba ndawona konse kutonza kwamakono kwa nyimbo, kunali momwe iwo ankachitira nazo; gulu la ma Ricky ataima pamenepo, akugwedezera manja awo mmwamba ndi pansi.

79 Ine ndithudi ndinamuyamikira mnyamata uja m'mawa uno, yemwe amaimba, amawoneka mwabwino, ngati mwamuna weniweni. Ine ndikuzikonda izo. Pamene Inu -

Inu amuna amalonda nthawizina kuno mumabweretsa gulu la ma Ricky awa omwe amaima kuno, ndi kukuwa ndi kufuula, ndi kumapitiriza, ndi kugwira mpweya wawo mpaka achite buluu pa nkhope pawo; ndipo uko si kuimba ayi, uko ndi kungopanga phokoso lambiri la mwa sayansi. Kuyimba ndi nthetemya zochokera mu mtima.

80 Ndipo ine ndinaganiza, "Nzachisoni bwanji! Ndi zamanyazi bwanji chomwe ziri! Kotero omwe pansi pa dzina la chipembedzo, iwo amachita ngati kuti kulibe Mulungu!"

Wina wake ananena, tsiku lina, kwa mnyamata yemwe akuyenda ndi mwana wanga wamkazi. Mnyamata wa ChiKhristu anati,(kupereka ndemanga yochenjera yokhudza Adamu ndi Hava), anati, "Hava akudutsa m'munda. Anati, 'Ana, inu mukuona mtengo uwo apo?' [anati,] 'Ndi pamene amayi anu anadya natitulutsa ife kunja kwa nyumba ndi kwathu.'" Kodi inu mungakhoze kulingalira, amayenera kuti akhale ali MKhristu wolimba, yemwe akanatenga lonjezo ndi Mawu a Mulungu ndi kuziponyera izo ku khola la nkhumba! Iwo amachita ngati iwo sadzati adzabwere ku Chiweruzo. Koma Mulungu adzabweretsa chinsinsi chirichonse pa Chiweruzo. Iwo amachita ngati kuti kulibe Mulungu.

81 Ine sindikufuna kuti ndiwatchule iwo zitsiru, chifukwa Baibulo linati… chitsiru si kukhoza. Yesu anati izo si ndizo… "Musamutchule munthu aliyense chitsiru." Koma mu Masalmo 14:1, "Chitsiru chimanena mu mtima mwake, 'Kulube Mulungu.'" Mukuona? Iwo, sali… Ine sindikufuna kuti ndiwatche iwo zitsiru, koma iwo amachita ngati iwo ali. Iwo amachita monga choncho.

Kotero, inu mukuona pamene ife tiri lero - ngati, "Kulibe Mulungu." "Ndine wa mpingo!" Ndipo chinthu chonsecho, Baibulo, ndi nthabwala yaikulu. "Mpingo wathu ukudziwa komwe iwo akupita!" Eya… Kulunjika kumene waku gehena, ndendende. Ali kumene pa njira yawo yomwe, akutsika kudutsa kupyola musayansi ndi maphunziro, maseminare a maphunziro azumulungu ndi zinthu, kumangowapemerera iwo akudutsa mu msewu. Mzimu Woyera sumakhala ndi mwayi woti upereke vumbulutso pa kalikonse; seminare yazidulira kale kunja izo. Mzimu Woyera ndi woti uzititsogolera ife; osati seminare, osati mabishopu ndi oyang'anira, ndi ena otero. Mzimu Woyera ndiye Mtsogoleri wathu.

82 Kaini anali munthu wotero monga choncho. Iye anali wachipembedzo kwambiri mu zochita. Tsopano ngati chipembedzo chiri chonse chomwe inu muyenera kukhala nacho ndiye mulungu anali wosalungama pa kumuweruza Kaini. Chifukwa, iye anali wachipembedzo, iye anali wachipembedzo basi ndi wodzipereka monga Abele analiri. Tsopano kumbukirani iye ankaganiza za Mulungu, iye ankamupembedza Mulungu, iye anali nawo mpingo, iye anamanga guwa, iye anapanga nsembe, iye ankapemphera, iye ankapembedza, koma iye anakanidwa. Ziribe kanthu motani…. Esau anali, nayenso. Mukuona? Chipembedzo, onani, imeneyo ndi ntchito ya Satana; osati kuti aphe chinthu chonsecho, koma kungochiipitsa icho. Ndizo zonse. Iye sangaphe chinthu chonsecho. O, osati chikominisi; ayi, wotsutsa Khristu si chikominisi. Baibulo linati, "Izo zikanati zidzanyenge Osankhidwa ngati kukanakhala kotheka." Musasamale zotchinga za zitsulo (iron Curtain), koma za chibakuwa (purple one).

83 Koma, zindikirani, Kaini anabwera kudzapembedza koma iye anali ndi mbewu yolakwika mwa iye, mbewu ya serpent. Mluzu wa serpent unali utalizira pa iye, pakuti iye anali mbewu ya mkazi. Iye ankadziwa chifuniro changwiro cha Mulungu, koma iye anakana kuti achite icho. Kodi inu mukudziwa zimenezo? Satana amachidziwa chifuniro cha Mulungu, koma iye amangokana kuti achichite icho.

Zindikirani, iye anali atamuwona Mulungu akutsimikizira uthenga wa Abele. Tsopano ine ndikufuna kuti inu muganize, mugwiritse ntchito Sefa yanu ya mwamuna woganiza tsopano kwa kamphindi. Uthenga wolondola wa Abele, umene Mulungu anautsimikizira kuti unali Choonadi! Kodi inu mukuchiona chithunzithunzicho tsopano? U - nhu. Uthenga wa Abele unali utalandiridwa, ndipo Kaini anaziwona izo ndipo anadziwa kuti Mulungu anali atautsimikizira uthenga umenewu ndiwolondola. Koma iye basi sakanachita icho. Kunyada kwake kunamuchotsa iye kwa izo. Uko nkulondola kunyada kwake

kunamulepheretsa iye kuchita izo. Iye anamuwona Mulungu akutsimikizira uthengawo.

84 Kotero izo zikuwoneka kuti ziri tsopano, zovuta kwambiri kwa anthu kuti adzichepetsere okha ku Mawu a Mulungu. Iwo, iwo samafuna basi kuti achite zimenezo. Iwo amadzichepetsera okha kukachikhulupiriro ka mpingo, zedi, koma osati ku Mawu a Mulungu. Ngati inu mukufuna kuti muzipeze izi, inu mupite ku…. Ine ndiri nawo Malemba pano, ndi omwe ine ndikuyang'ana pano. Genesis 4:6 ndi 7, Mulungu ananena kwa Kaini, anati, "Chifukwa chiani nkhope yako yagwa? Chifukwa chiani iwe uli yense wodzaza ndi kupsyamtima, nkumayenda yenda? Iwe wangomva uthenga umene wakukwiyitsa iwe." Anati, "Chabwino, iwe ukuchitira chiani izo? Chifukwa chiani nkhope yako yagwa, chifukwa Ine sindinabwere ku tchalicthi chako? Kotero chifukwa chiani iwe unachita izo? [Kodi inu mukugwiritsa ntchito Sefa ya mwamuna woganiza?] Mukuona? Kapena, "Bwanji sunati….bwanji iwe ukuwoneka monga choncho?" Anati, "Ngati iwe uti uchite bwino, pita ukachite momwe m'bale wako akuchitira kunja uko, Ine ndikulandira iwe ndipo ndikudalitsa iwe. Ine ndikuchitira iwe chinthu chofanana." Koma iye sakanakhoza basi kuzichita izo. Iye anati, "Tsopano, ngati iwe sutero, tchimo la kusakhulupirira lagona pakhomo."

85 Tsopano pamene iwo akutiuza ife, "Masiku a zozizwitsa anapita." Iwo nkumaziwona izo zikuvomerezedwa mwangwiro kwambiri ndi kumatsimikiziridwa, inu mukuona, zinthu zonse izi zomwe Mulungu analonjeza kuti Iye akanati adzachite mu masiku otsiriza, za Chivumbulutso 10 ndi Malaki 4, zinthu zonse izo zitatsimikizidwa mwangwiro kwambiri. Chavuta ndi chiani, abale? Chalakwika ndi chiami, mwaona? Ngati iwo satero; kusakhulupirira, komwe kuli tchimo. Liripo tchimo limodzi lokha, ndilo, kusakhulupirira. Zoona zimenezo. Inu simumaweruzidwa chifukwa inu mumamwa, kusuta, kutafuna, kuvala zazifupi, kuchita chirichonse chimene inu mumachita. Ayi, izo sizimakuweruzani inu. Ndi chifukwa chakuti inu simumakhulupirira. Ngati inu mukanati muzikhulupirira, inu simukanati muzichita izo. Mwaona? Wokhulupirira samachita zimenezo. Iye amatenga Sefa ya mkazi woganiza, iliyonse ya iwo. Chabwino. Koma, inu mukuona, tchimo lagona pakhomo.

86 Tsopano zindikirani chomwe izo zinachita kwa Kaini, ndipo izo zikhala ziri zofanana lero. Izo zinamupangitsa Kaini kupita kwina, wochimwa mofuna dala. Iye mwakufuna anali wosamvera. Munthu aliyense adzakhala mwanjira yomweyo. Mwakufuna iye sanamvere atatha kuwuwona uthenga wa Abele ukutsimikiziridwa kwambiri ndi Mulungu, kuti iwo unali woona, ndipo anakana kuti achite izo. Anachita chinthu chofanana ndi chimemnecho.

Ndiye iye anawoloka mnzere wolekanitsa. Pali mzere umene ungakhoze kuwuwoloka. Inu mukudziwa zimenezo, sichoncho inu? [Osonkhana akuti, "Ameni." - Mkonzi.] Tsopano, atumiki, nonse kuno ndi kunja dziko la lamya kumene kulengeza uku kukubwera kudutsa fukoli, kodi mukuzindikira zimenezo? Pamene inu muwona kuti izo ndi Lemba, ndipo inu nkusachita izo, Mulungu sangathe nthawi zonse…. Iye adza…. O, inu muzipitirira kumadalitsidwa. Chotero anali aliyense wa Israeli, iwo ankakhala mu chipululu momwe, ndi kumalera ana, mbewu, ndi kumadalitsidwa, ndizina zonse, koma "aliyense wa iwo atalekanitsidwa kwaMuyaya ndi Mulungu." Yesu ananena chomwecho. O, inde, Mulungu azikudalitsani inu mopitirira basi, koma inu mwapita. Ndithudi. Ndi chimene Baibulo likunena tsopano, ndi chimene Iye ananena.

Zindikirani, inu mukhoza kuwoloka mzere wolekanitsa. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Kaini anachita zimenezo.

87 Tiyeni - tiyeni tingotembenuzira apa mphindi, ine ndiri ndi Ahebri 10:26. Tiyeni tiwone ngati ine ndingazipeze izo mwamsanga momwe. Buku la Ahebri, mutu wa 10 ndi….ine ndikukhulupirira, ndime ya 26. Ine ndinazilemba izo pano. Mphindi yokha, ngati inu mungapirire ndi ine, ndipo tiyeni tingowawerenga Iwo mphindi chabe. Chabwino, ndi ife apa.

Pakuti ngati ife tichimwa dala pambuyo pa kuti ife… titalandira chidziwitso cha Choonadi, sipatsalanso nsembe ina ya kwa tchimo,

Koma mawonekedwe ena owopsya a chiweruzo ndi ukali woopsya, umene uti udzamuwonenge mdaniyo.

Ndizo PAKUTI ATERO MAWU OYERA A MULUNGU. Ngati ife sitikukhulupirira mwadala pambuyo pa kuwawona Iwo ndi kuwamva Iwo, ndiye ife tawoloka mzere. Apo sipadzakhala konse chikhululukiro china kwa izo, inu mwaoloka mzere.

"O," inu muziti, "Mulungu akudalitsabe ine." O, eya.

88 Kumbukirani Israeli, mizere ya mmalire. Pamene Mulungu anawapatsa iwo lonjezo, uko mu Dziko Loyera; mu dziko, ilo linali labwino, la mkaka ndi uchi. Ndipo pamene Mose anamutuma Kalebu ndi Yoswa, ndi azondi, kuti apite ndi kukalizonda dzikolo, ndi kubweretsa mmbuyo umboni wotsimikiziridwa. Khumi a iwo anati, "Ife sitingakhoze kuzichita izo. Ndife osakhoza. Tayang'anani pa zovutazo apo. Ife tikhala tiri otentheka. Ife tiri nazo zinthu zazing'ono kwambiri izi zoti timenyere nazo. Taonani zomwe iwo ali nazo. Ife, ife sitingakhoze kuchita izo. Ife sitiri okhoza kuzichita izo."

Yoswa ndi Kalebu anati, "Ife ndife oposa kukhoza kuzichita izo! Mulungu anapanga lonjezo." Ndipo,

kumbukirani, iwo anatembenukira m'mbuyo. Apo panali pa Kadeshi - Barnea. Ndipo iwo anabwerera m'mbuyo ndipo anakhala oyendayenda mu chipululu. Ndipo aliyense wa iwo anafa, ndipo anataika kwaMuyaya. Yesu ananena chomwecho. Musadutse mzere wolekanitsa uwo, onani. "Pamene inu mukudziwa kuchita bwino, ndipo nkusamakuchita iko, kwa inu ilo ndi tchimo."

89 Israeli anachita mofanana. Iwo atamuwona kale Mose kuti watsimikiziridwa, ndiyeno nkudzamulola Balaamu kuwapemerera iwo, Mbewu yofunika yotsimikiziridwa iyo. Abusa, inu musati (nkomwe) Musanene kanthu kowatsutsa Mawu awa. Tayang'anani pa Balaamu, iye anali mneneri, ndipo iye anaiwona Mbewu ya Mulungu, ikutsimikiziridwa. Koma pansi pa chipembedzo chake chomwe chachikulu chomwe iye ankakhalamo, Moabu ataliwona gulu lija la oyenda yenda akubwera kudutsa mu dzikolo, iye analipemerera iro, ndipo anati, "Chabwino, dikirani mphindi. Ndife tonse AKhristu. Ndife tonse okhulupirira. Moti makolo athu ndi makolo anu ndi ofanana. Kodi sindife ana a Loti? Kodi sanali Loti, mdzukulu wa Abrahamu? Kodi sindife tonse ofanana? Tiyeni tizikwatirana wina ndi mzake."

Ndipo Israeli, monga Eva mmunda wa Edene, anamulola Satana kupemerera pa iye, iye anapemereranso pa Israeli kupyolera mwa mneneri wabodza. Pamene, mneneri weniweni anali ndi iwo, ali nawo Mawu otsimikiziridwa. Koma mwa kudziwa kwa chidziwitso chaluntha, iye anawapemerera iwo. Taganizani za izo.

Tsopano, izo sizinakhululukidwe nkomwe, tchimolo silinakhululukidwe nkomwe.

90 Mbewu zinavundira mu njira ya ntchito momwemo, pa ulendo waku dziko lolonjezedwa. Aliyense wa iwo anawonongeka ndipo anavunda, molunjika kumene mu mpingo, mu mzere wa ntchito, akumutsatira Mulungu. Ndipo anamulola Satana kuti apemerere mpemera waluntha uwo pa iwo, wamaphunziro, kudziwa kwa luntha, kumati, "Bwanji, ife tonse ndife amodzi, ndife tonse ana a Mulungu." Inu simuli!

Koma iye anamulola mphunzitsi wabodza uja uko awapemerere iwo ndi lingaliro laluntha ilo lomwe iye anali nalo pa Iwo. Ndipo basi momwe aBungwe la Mgwirizano likuchitira pakali pano, onani, chinthu chofanana, "Bwanji, ife tonse tilumikizane limodzi mu bungwe limodzi lalikulu." Kachitidwe kanu konse kachi bungwe ndi ka mdierekezi. Ndi chilemba cha chirombo, mu Baibulo. Ine ndikhala nalo buku pa izo, posachedwa apa, Ambuye akalola.

91 Zindikirani, inu nthawi ya Nowa, powaona Mawu ali kumangidwa, kuti ayandame. Tsopano ndiloleni ine ndipange ndemanga yaing'ono pano, Mawu akuikidwa palimodzi kuti asinthidwe kuchokera ku nthaka kupita mu mlengalenga. Akuwona chimango cha chinthucho; koma ali ndi kumvetsa kwawo kwa luntha, anasekedwa pamaso pa mneneri Noah pamene iye anali nkunenera za nthawi yo maliza.

Koma nchiyani chi … Chimangocho chinapangidwa ndi Mawu a Mulungu, chitamatidwa mkati ndi kunja ndi pemphero nd chikhulupiliro. Pamene mvula inabwera, zoganiza zonse zaluntha za zipembedzo zinafa ndipo zinavundira umo momwe… mu mipingo yawo momwe, pa dziko lapansi pomwepo. Ndipo chombo chinayandama pa mwamba pa izo zonse. Mbewu zopemereredwa mwasayansi zinavundira mu chiweruzo chomwecho.

92 Kodi ife tikuyesera kuchita chiani, mulimonse, kodi ife tikuyesera kuti tikhazikitse mpingo wathu kapena kodi ife tikuyesera kuti tikhazikitse Mawu a Mulungu? Kodi ife tikuyesera kumachita chiani? Kodi ife tikugwira ntchito pa chiani? Kodi ife tikuyesera kuti tiwabwezere anthu m'mbuyo mu Ichi? Kodi Hava wamkulu uyu akuyesera kuchita chiani pano mu masiku otsiriza ano, Hava wa mpingo uyu?

Ine ndiyenera kuti ndisiye pakali pano pomwe, m'bale, chifukwa ta - tayamba kuchedwa kwambiri. [M'bale akuti, "Pitirirani!" - Mkonzi.] Ingondipatsani ine pafupi mphindi khumi ndi zisanu zowonjezera, ndipo ine ndiimira pa anga - Malemba anga apa. ["Ndithudi, pitirirani."] Eya. Chabwino. Ine ndikudziwa. Chabwino, anthu mwinamwake akufuna alowe muno ndi kudzasesamo muno. Koma ine ndikungowoneka ngati kuti izi ndi zovuta kwa ine kuti ndizisiye. ["Ingopitirirani." "Chabwino, apo palibe chofulumirira."] Ine ndifulumira.

Chabwino.

93 Taonani, sayansi yaikulu, ya maphunziro, Hava wahaibridi lero, wotchedwa mpingo, kodi iye akuyesera kuchita chiani? Kodi iye akuyesera kuti awakuze Mawu a Mulungu, ndi kumawalola anthu kuti azichita momwe iwo akuchitiramu? Iwo sakugwiritsa ntchito Sefa ya mwamuna woganiza, kapena, Sefa ya Mulungu. Taonani zomwe iwo akubala. Iwo akumadzikweza okha. Mpingo uli, mu madongosolo ake achidziwitso a mbewu yolumala, zapangitsa mtundu wonse kuti ukhale mbuli mwasayansi ku Mawu a Mulungu. Tsopano ine ndizigwira ndemanga izo, ine sindizigwira izo motalika kwambiri tsopano, kuti ndifike potsiriza. Mbuli mwasayansi! Pamene Mulungu, pomwe pano pa dziko lapansi, akuchita zinthu zomwe Iye akuzichita, mwa Mawu Ake olonjezedwa, ndipo iwo sakuzilabadira Izo ndi kuchokapo chifukwa iwo ndi mbuli mwasayansi. Mbuli mwasayansi!

94 (Ine ndinali kumwetulira apo chifukwa cha M'bale Williams pano, analemba pomwe pano pa chidutswa cha pepala, "Inu mukhoza kukhala pa izo madzulo onse," chinachake. Koma, ine ndikuyamikira izo, ndi

zabwino kwenikweni.)

95 Koma anthu ali - akumachimwa mwadala. Izo zabweretsa ka - kachitidwe konse ka dziko la mpingo lero mu tchimo ladala motsutsana ndi Mulungu. Bwanji, khalidwe wamba lingatsimikizire kwa inu kuti Izo nzoona.

Chabwino. Chotchinga chosirira chinachititsa khungu maso ake, kwa Mawu a Mulungu, ndipo iye akudzipeza yekha wamaliseche kachiwiri. Inu mukudziwa, Mulungu mu Chivumbulutso 3, anati, "Bwerani, mudzagule mankhwala opaka mmaso kwa ine, kuti maso anu akhoze kutsegulidwa." Mwaona, mankhwala opaka mmaso ndi Mawu Ake.

96 Inu mukudziwa, iwo amati, "Chabwino, munthu uyu anaphunzira kwa zaka makumi anayi, kuti apeze madigirii ake. Iye ndi B.L.D., D.D., ndi zonse izi."

Inu mukudziwa, zomwe Yesu ananena za izo? Iye anati, "Mwamuna adzikane yekha." Paulo anatero.

Inu mukuti, "Izo sizikutanthauza zimenezo." Chabwino, nchifukwa chiani Paulo amazitsatira izo, ndiye? Iye anati, "Ine sindinabwere nkomwe kwa inu ndi mawu odolola a nzeru za munthu chifukwa inu mukanati mumange ziyembekezo zanu pa izo. Koma ine ndabwera kwa inu mu mphamvu ndi mawonetseredwe a Mzimu Woyera, kuti mawu anu akhoze kukhala… chikhulupiriro chanu chikhoze kumangidwa pa Mawu a Mulungu, osati mawonetseredwe a nzeru."

97 Izo zikuoneka kuti anthu ataya chikhalidwe ndi ulemu wao. Iwo Sali, monga momwe analiri. Izo zinali mwakuti, pamene mneneri ankati, "PAKUTI ATERO AMBUYE," anthu ankanjenjemera. Eya, iwo ndithudi amkatero. Anthu ankasuntha, pakuti iwo ankachita mantha. Koma tsopano iwo ataya mantha awo onse kwa Iwo. Iwo sakumuwopa Mulungu.

Solomoni anati, "kuwopa Mulungu ndicho chiyambi cha nzeru," chiyambi chabe cha iyo.

Koma mneneri akhoza kuyankhula PAKUTI ATERO AMBUYE;

Anthu nkumati "zamkutu!" mwaona, palibe chiyembekezo kwa iwo. Ndizo… iwo amati, "Bwanji, ife ndife anzeru. Ndife aluntha, ife sitisowa kuti tizitenga zinthu za mtundu umenewo! Ife tikudziwa zomwe ife tikuziyankhula!" Palinso mwambi wakale, kuti, "Zitsiru zimayenda ndi nsapato zagogoda, pamene Angelo amawopa kupondapo." Ndithudi.

98 Tsopano, kodi kusandulizika ndi chiani? (mwamsanga.) ife timakupeza bwanji iko? Nchiani chimachititsa kusandulizika? Mulungu anachita iko mwa Mzimu wa Mawu Ake. Iye amasanduliza. Iye amabzala Mbewu Yake, amaponyera Mzimu Wake pa Iyo imabala zipatso. Mzimu Wake Woyera umasanduliza Mbewu ya Mawu nkati kuti itsimikizire za mtundu wake. Ndi mtundu wanji wa mbewu yomwe inu muli, izo zimangosonyeza zomwe ziri mwa inu. Inu simungakhoze kuibisa iyo. Chirichonse chomwe inu muli mkatimo, icho chimasonyezera kunjako. Inu simungakhoze basi kubisala kwa izo. Inu simungakhoze basi kuwupanga mtengo uwo kukhala chirichonse kupatula chomwe iwo uli. Mwaona, Iwo - iwo ukhala uli mwanjira imeneyo.

Mzimu Woyera umasanduliza mbewu zomwe ziri, mkati mwakemo. Ziribe kanthu mtundu wa mbewu zomwe ziri, Iwo umazisanduliza izo. Ngati ziri zoipa, izo zimadzabala zoipa. Ngati ili yachinyengo idzabereka yachinyengo. Ngati ziri Mawu enieni a Mulungu, izo zimadzabalapo mwana wamwamuna weniweni kapena wamkazi wa Mulungu, kupyolera mu Sefa ya mwamuna woganiza. Pamene Mbewu itulukirapo, iyo imatulukira kudzera mu Iyo, Iyo imabala mwana wamwamuna ndi wamkazi wa Mulungu.

99 Tsiku lina pamene dziko linali mu mdima wa chisokonezo, Mulungu… Tsopano mvetserani mwatcheru, chifukwa ife sitiyankhula… basi kungotalikitsa pang'ono. Penyani. Tsiku lina pamene dziko linali kachiwiri mu mitundu yonse ya zipembedzo, kusamba mmanja, mipoto, kuvala mikanjo yosiyanasiyana ndi zibenenga, ndi zina zotero, ilo linali mkati mwa chisokonezoko chathunthu. Israeli weniweni wa Mulungu anali atapotozedwa nachoka ku malamulo ndi malangizo a Mulungu, Yesu anati, "Inu ndi miyambo yanu, mumawapangitsa Mawu a Mulungu kukhala opanda chochita kwa anthu, mwa miyambo yanu." Ndipo tayang'anani pa ansembe oyera awo, omwe iwo ankawatcha; ndipo Yesu anati, "Inu ndinu a atate wanu, mdierekezi, ndipo ntchito zake inu mukuzichita." Mwaona, ndi ndendende zomwe Iye ananena.

100 Tsopano pamene dziko linakhala mu chikhalidwe cha mtundu umenewo, Mzimu wa Mulungu unasinthira kachiwiri pa Mbewu yomwe inakonzedweratu. Iye anamasulira ndi kusintha Yesaya 9:6 pa za lonjezo Lake; Iye, Mulungu, anapangidwa mu mnofu wa umunthu, kuti ayipulumutse nthawi ya chisokonezo iyo. Pamene munthu anapangidwa mu chifanizo cha Mulungu, apa pakubwera Mulungu, mwa mneneri atapenyeratu izo…. Tsopano kumbukirani Mawu, mneneri anaziwoneratu izo, mneneri yemweyo basi yemwe anamuwona Satana mu masiku otsiriza ano, mwaona, wa dongosolo la maphunziro ili ndi zinthu zomwe iye ali nazo, dongosolo la za chipembedzo. Mneneri yemweyo, Yesaya 9:6, anati, "Kwa ife Mwana wabadwa, kwa ife Mwanawamwamuna waperekedwa; ndipo Dzina Lake azidzatchedwa 'Wauphungu, Kalonga wa Mtendere, Mulungu Wamphamvu, Atate Wosatha.' Ndipo ku ulamuliro Wake

sikudzakhala mapeto." Ndipo Mawu awo anali Mawu a Mulungu. Ndipo Mzimu unasunthira pa Mawu amenewo, ndipo Iwo anawumbidwa mu chiberekero cha namwali; Mwamuna, "Mwanawamwamuna wabadwa," osati walengedwa, "wabadwa."

101 Satana anayesera ndi kuyeseranso kuupemerera Iwo. Iye amutengera pamwamba ndipo anati, "Ngati Iwe uli chimene Iwe ukuti Iwe uli, ndiye chita zina za machiritso awa pano kwa ine. Ndisonyeze ine momwe Iwe ungakhoze kuchitira izo. Sandutsa mkate uwu, ndi miyala iyi ikhale mkate. Tiye tikuwone Iwe ukudziponyera pansi, chifukwa Lemba limati Iwe udzachita izo." Inu mukuwona adierekezi a chipembedzo awo lero akumanenabe chinthu chomwe chomwecho? "Ngati pali chinthu chotero ngati machiritso Auzimu; apa pagona M'bale Wakuti - ndi - wakuti, tiye tikuwone iwe ukumuchiza iye."

Mdierekezi yemweyo anaima kwa Yesu, pa mtanda anati, "Ngati Iwe uli Mwana wa Mulungu, tsika kuchokera pa mtandapo." Mawu anati Iye anali Mwana wa Mulungu. Mzimu unatsimikizira kuti Iye anali Mwana wa Mulungu. Yesaya 9:6 anakwaniritsidwa. Ndipo usiku wina, ambiri a inu mu kuwulutsa mawu munamva momwe ife timaperekera Malemba - ena - osamvetsetseka - makumi asanu ndilimodzi, pafupifupi, ine ndikukhulupirira, otsimikizira kuti Lemba linanena kuti Uyo anali Iye.

102 O, Satana anayesera ndi kuyeseranso, kuchita chirichonse. Usiku wina, atagona kumbuyo kwa ngalawa, iye anamuwona Iye atagona. Ndipo iye anati, "Ine ndimuwononga Iye pakali pano." Koma iye sakanakhoza. Iye anayesera kuti amuyese Iye kuti achite chinthu cholakwika, koma iye sakanakhoza kuchichita icho. Bwanji? Iye anali atapemereredwa ndi zobweza mphamvu za kukonzedweratu. Izo sizingangakhoze kunyengedwa. Ayi, ayi. Mawu anati Iye akanadzakhala ali pano. Ameni. Palibe mdierekezi ati amuvutitse Iye, ndipo palibe mwana wina wa Mulungu, yemwe anakonzedweratu kuti adzatenge malo ake. Iye anapemereredwa ndi zobweza mphamvu. Chiphe cha Satana, madotolo achipembedzo samamukhudza Iye nkomwe konse. Iye amangosuntha mopitirirabe, palibe chomwe chiti chimuvutitse iye, mwaona. Izo zinalibe chochita chirichonse pa Iye.

103 "Chabwino, ine ndikupanga Iwe ukhale bishop wa dziko lonse lapansi. Ine ndiri ndi ulamuliro pa ilo. Ngati Iwe uti undipembedze kokha ine, tiyeko dzajowine gulu langa, ine ndi- ine ndikupanga Iwe kukhala wolamulira. Ine nditsika, nkulola Iwe ukwerapo."

Iye anati, "Pitani kumbuyo Kwanga, Satana. Zinalembedwa kuti, 'Iwe uzipembedza Mulungu, Mawu, ndipo Iye yekha iwe uzimutumikira.'"

Ndiye tsiku lina (Pa Munthu wamkulu uyu, ine ndikufuna kuti ndikhale pamenepo kanthawi.)…Koma tsiku lina, Mzimu unasunthira pa Iye kachiwiri; chifukwa panali Mawu ena omwe analembedwera za Iye, ochokera kwa Mulungu, kupyolera mwa mneneri, "Ndipo Iye anatsogozedwa kuti akaphedwe, monga mwanawankhosa." Ndipo Mzimu unasunthira pa Iye, ndipo unamutsogolera Iye, ndipo unamutumiza Iye ku mtanda wa pa Kalvare. Pamenepo Iye anafa. Ndipo chirichonse chimene chinayankhulidwira za Iye mu imfa Yake, chinakwaniritsidwa, kuti abweretse Kuwala ndi Moyo kwa mbewu yonse yokonzedweratu ya Mulungu yomwe inali pa dziko lapansi. Iye anabweretsa njira yochitira izo. Apa pali Mbewu, Mzimu umabweretsa Moyo; kuwasanduliza ana a amuna ndi a akazi a Mulungu, kuchokera ku dziko mu chisokonezo cha mdima ichi, kukalowa kuti akakhale ana aamuna ndi aakazi a Mulungu.

104 Musapunthwe pa mawu awo akuti "kukonzedweratu." Ine ndikudziwa kuti inu mukutero. Koma, mvetserani, Awo si mawu anga. Awo ndi amodzi a Mawu a Mulungu. Inu mukufuna kuti muwawerenge iwo, werengani Aefeso 1:5, pomwe, "Iye anatikonzeratu ife kuti tidzakhazikitsidwe monga ana Ake kupyolera mwa Yesu Khristu." Mwaona.

Mungondilola ine ndiziswe izo phindi yokha, mphindi yokha, kuti ndiziswe izi zichoke mu malingaliro anu. Taonani. Basi monga inu munali mwa atate anu, pa chiyambi, (mbewu ya nyongolotsi. Kodi inu mukudziwa zimenezo, aliyense wa inu?)Inu munali mwa agogo - a agogo - a agogo anu aamuna, aponso, kodi inu mumadziwa zimenezo?

Werengani Buku la Ahebri, kumene ife tikupeza kuti Levi anapereka chakhumi pamene iye anali mchiuno cha Abrahamu, mibadwo inai mmbuyo mwa iye. Pamene Abrahamu anapereka zakhumi kwa Melkezedeki, izo zinawerengedwa kwa chidzukulu cha chidzukulu cha chidzukulu chake m'musi umo kwa iye, ndipo iye analipo apo mu chiuno cha Abrahamu.

Ndi zimenezotu, Mwaona.

105 Inu munali mu chiuno cha abambo anu, koma abambo anu sakanakhoza kukhala ndi chiyanjano chirichonse ndi inu mpaka inu mutasandulizidwa kukhala thupi la mnofu. Mwana wanga apo anali mwa ine. Ine - Ine - ine ndinkafuna mwana, koma iye anali mwa ine pamenepo. Mukuona? Iye anali mwa ine apo. Koma kupyolera mu chikwati, iye anasandulizidwa kudzakhala mwamuna monga ine, ndiye iye anadzakhala monga ine. Ndipo inu munadzakhala monga makolo anu, mwaona, chifukwa izo zinali mwa inu, poyamba pomwe.

Tsopano ngati ife tiri ana a Mulungu, zikhumbo Zake…. Chimene, inu muli chikhumbo cha bambo anu,

osati amayi anu; bambo anu. Nyongolotsi imakhala mwa bambo. Mwaona? Ndipo tsopano mayi anu anali ofungatira chimene chinakubalani inu, chinabala mbewu ya bambo anu. Mwaona.

106 Ndipo dziko lapansi, mwa thupi, nalonso ndi chofungatira chimene chimabala mbewu ya Mulungu. Mwaona, chimodzimodzi basi. Osati dziko, momwe dziko liriri lalikulu; ndi momwe aliri wamkulu Mulungu yemwe analipanga ilo, Mukuona.

Tsopano ngati inu muli mwana wa mwamuna ndi wamkazi wa Mulungu, ndiye inu munali mwa Mulungu pachiyambi. Ndinu chikhumbo Chake. Ngati inu simunali uko apo, ndiye kuti inu simunali konse kapena simudzakhalakonso konse. Chifukwa, ine sindingakhoze kubala, kuchokera mu chiuno changa, mwana wa bambo uyu apa kapena bambo uyo apo, ine ndingakhoze kokha kubala ana anga omwe, ndipo iwo azikhala nawo mawonekedwe anga. Aleluya. Inu mukuziona zimenezo?

107 Ana a amuna ndi a akazi anali mwa Mulungu pachiyambi.

Tsopano taonani. Inu muli nawo Moyo Wamuyaya, inu mukutero. Ife tikukhulupirira zimenezo, kuti ife tiri nawo Moyo Wamuyaya. Chabwino, alipo mawonekedwe amodzi okha a Moyo Wamuyaya, ndipo uyo ndi Mulungu. Ngati inu muli nawo Moyo Wamuyaya, Moyo umenewo umene uli mwa inu unalipo nthawizonse, ndipo inu munali mu chiuno cha Mulungu pasanakhale ngakhale dziko.

Ndipo pamenepo Mawu pawokha…. Yesu Mwiniwake amatchedwa Mawu, ndipo mu Yohane Woyera 1, anati, "Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu." Ndiye inu munali mu chiuno cha Yesu, ndipo munapita ku Kalvare limodzi ndi Iye. Inu munafa ndi Iye, ndipo inu munauka ndi Iye. Ndipo lero ife tikukhala mu malo a Mwambamwamba mwa Iye, mutadzadzidwa ndi Mzimu wake, ana a amuna ndi a akazi a Mulungu. Tinafa ndi Iye, tinauka ndi Iye. Zedi.

108 Tsopano ndiye, tsopano, inu mukhoza kuyanjana naye Iye. Inu simukanatero m'mbuyomo uko, chifukwa inu munali Mawu chabe mwa Iye, mbewu. Koma tsopano Iye wakuwonetserani inu, ndipo tsopano Iye akufuna kuti Inu mudziyanjana naye Iye. Ndiye Iye anatsika, anadzapangidwa thupi chotero kuti Iye akanakhoza kumayanjana mwangwiro ndi inu. Mukuchiona chiyanjano changwirocho? O, mai, zinsinsi zakuya za Mulungu izo! Kudabwitsa kwake!

Mwaona, Mulungu sangakhoze kuchita chiyanjano mu Mzimu, kotero Mulungu anadzakhala munthu limodzi nafe. Yesu Khristu anali Mulungu Mwiniwake, woonetseredwa, chifukwa, Iye anali mwana chifukwa Iye anachita kubadwa, koma Iye anangokhala kachisi woti Iye adzikhalamo. "Palibe munthu anamuwonapo Mulungu panthawi iliyonse, koma wobadwa yekhayo wa Atate wa muwonetsera Iye." Mulungu anadzimangira yekha nyumba, thupi kuti azikhalamo, anatsika chotero kuti inu mudzikhoza kumugwira Iye. Timoteo oyamba 3:16, "Popanda kutsutsana, chinsinsi cha umulungu ndi chachikulu; pakuti Mulungu anawonetseredwa mu thupi, anawonedwa ndi Angelo… anakhulupiriridwa… analandiridwa M'mwamba." Mwaona?

Tsopano Iye….

109 inu pokhala mnofu, ndi Iye pokhala mnofunso, ndiye inu mukhoza kumayanjana tsopano, chifukwa Iye anali chikhumbo cha Mulungu chachikondi. Mulungu ndi chikondi. Ndikulondola uko? Ndipo Yesu anali chikhumbo cha Mulungu cha chikondi. Ndipo pamene chikhumbo chachikondi chinawonetseredwa. Chimene, uyo anali Mulungu Mwiniwake; zikhumbo zonse zomwe zinakanirira mwa Iye, zinadza kwa Iye, "Onse amene Atate andipatsa Ine, adzadza kwa Ine." Zedi, iwo akanayenera kukhala ali okonzedweratu. Ngati izo sizinali, inu simukanati mudzakhalepo apo. Ndizo zonse. Ndithudi.

Tsopano ife tikhoza kumayanjana, zinali kupyolera mu - mukulemera kwa Mawu Ake, ndichomwe inu muli gawo lake. Inu ndinu gawo la Mawu; chifukwa Iye anali Mawu pachiyambi, inu ndinu Mawu pano. Mwaona? Ine ndikulalikira usiku uno, kapena Lamlungu kapena limodzi la masikuwa pamene ine ndidzalowamo, pachomwe Mawu ali, mwaona. Ndipo tsopano inu ndinu gawo la Mawu.

110 Mvetserani. Pali chinthu chimodzi chimene ine sindingakhoze kuchichita. Ine sindingakhoze kuzitamandira kwa Makolo anga omwe anapita. Ayi, ine ndinabwera kupyolera mu nyasi zoipa. Bambo anga anali achi Irish. Amayi anga anali Achimwenye okwatiwa ndi nzungu, theka Mmwenye; Amayi awa anali Mmwenye, ankalandila ndalama za peshoni. Tsopano, onse a iwo, zidakhwa, pafupi ambiri a iwo anafa atavala nsapato zawo, pomenyana, andewu za mfuti, ndi zina Zotero. Ine sindingakhoze kuzitamandira pa kalikonse ka izo, chifukwa makolo anga omwe anapita ndi m'ndandanda wa banja langa ndi oipadi. Koma, M'bale, pali chinthu chimodzi chomwe ine ndingadzitamandirepo, ine ndikhoza kudzitamandira pa Ambuye wanga Yesu Yemwe wandiwombola ine. Ndipo ndi mphamvu Yake yosanduliza anabzala mbewu, mwakukonzedweratu, ndipo ine ndinaiwona Iyo. Ndine mwana wa ndani tsopano? Eya. Ine ndikhoza kudzitamandira pa Iye. Ndipo ine ndakhala zaka makumi atatu ndi zitatu za moyo wanga, ndikudzitamandira pa Iye. Ngati Iye angandisunge ine zaka zina makumi atatu ndi zitatu, ine ndiyesera kudzitamandira mochuluka pa Iye. Mwaona? Ine ndikhoza kudzitamandira pa kholo langa, Aleluya!

Iye yemwe anandiwombola ine ndipo anabzala mbewu ya moyo mkati umu, ndipo anandilola ine kumayang'ana apa pa Mawu awa, ananditumizira kuno Mzimu Wake ndipo anati, "Ndi Uwu pano. Lankhula ichi, ndipo zichitika. Chita icho." Ndipo O, mai, ine ndikhoza kudzitamandira pa Iye! Kodi Iye anachita motani izo? Kupyolera mukutsuka kwa madzi a Mawu, madzi olekanitsa. Ndikanakhumba tikanafotokoza izo.

111 Okhulupirira owona okonzedweratu azakhalabe ndi Mawu chifukwa iwo ali gawo la Mawu amenewo.

O, nyenyezi zoyendayenda, muziyendayenda mpaka liti? Inu Achimethodisti, Achipresbateria, akunja, chirichonse chomwe inu mungakhoze kukhala muli, - nyenyezi zoyendayenda, kuchokera ku mpingo kupita ku mpingo, kuchokera ku nsanamira kupita ku malo, ndi televizioni kupita ku televizioni, dziko kupita ku dziko, bwanji inu osangobwerako? Iye akukhumba kuti akhale ndi chiyanjano ndi inu. Iye akukukhumbani inu.

Iye akufuna kuti akusintheni inu mwa kukonzanso kwa malingaliro anu, osati kwa mpingo kapena kwa chipembedzo, koma kwa Mawu Ake, omwe, inu muli gawo lake ngati chokhumba icho chiri mwa inu.

Odala ali iwo omwe akumva njala ndi ludzu la chilungamo: pakuti iwo adzakhutitsidwa, (mwaona) Ndipo watumiza mphamvu Yake yosanduliza, kuti akuchotseni inu mu kulumala uku kwa chipembedzo komwe inu mulimo. Mu chisokonezeko cha kulumala ichi chomwe ife tirimo, Mulungu watumiza Mphamvu Yake yosanduliza, Mawu Ake, ovomerezedwa, otsimikiziridwa, kuti akutulutseni inu mu kulumala kwa chipembedzo uku kwa umbuli komwe inu muli kuyendamo, "amaliseche, akhungu, omvetsa chisoni, ndi opanda kudziwa izo." Tagonizani za izo, abwenzi.

112 Inu mukudziwa, Mulungu anatumiza mphamvu Yake yosanduliza kuti akwaniritsire Mawu Ake, ndipo anasintha thupi lonse la Sarah ndi Abrahamu. Anamusanduliza munthu wokalamba ndi mkazi wokalamba, chifukwa Iye analonjeza kuti Iye akanadzachita izo. Ndipo chimene Mulungu alonjeza kuti achita, icho Iye amachichita. Palibe kanthu, kalikonse… Chinthu chosokonezedwa chirichonse, Mulungu sangakhoze kuchita kanthu ndi icho. Koma Iye adzasunga Mawu Ake, ndipo Iye adzatumiza Mzimu Wake! "Ine Ambuye ndaubzala Iwo. Ine ndizauthirira Iwo usana ndi usiku, kuwopa kuti ena angaukhwathule iwo kuchokera m'manja Mwanga." Baibulo limanena zimenezo.

113 O, nyenyezi zoyendayenda, inu omwe muli ndi chikhumbo mu mtima mwanu - Inu muyenera kuti muli nacho icho, kapena inu simukanati mukhale pano mmawa uno. Ndipo inu simukanati mukhale mu mipingo iyo ndi mnyumba zoyankhuliramo, ndi zinthu zomwe inu mulimo, uko ndi kudutsa mu dzikoli, ngati china chake chikanati chisakubweretseni inu mmenemo. Munthu wina anayankhula kwa inu. Musapite pa tsogolo paliponse. Pali kutsuka kwa madzi mwa Mawu, kumene kuti kudzakupangeni inu kuyera monga chipale. O, ana a Mulungu, mvetserani! Musakhale mu kulumala uko. Tulukanimo umo. Abrahamu anamukhulupirira Mulungu, ndipo anachitcha chirichonse chosiyana…Inu mukuti, "Ine ndingamakhale bwanji moyo? Ine ndingamachite motani izi?" iyo ndi ntchito ya Mulungu. "Ine ndingati? Oyanjana nawo anga angandikane ine."

Mulungu anati, "Iye yemwe ati adzawasiya abambo ake omwe, amake, mkazi wake, mwamuna wake, kwawo, manyumba; ine ndidzawapatsa kwawo ndi manyumba, ine ndidzawapatsa iwo abambo ndi amayi, ndi abale ndi alongo, mudziko lino, ndi Moyo Wamuyaya mudziko likudzalo. Ilo ndi lonjezo, mzanga. Kuti, o, izo ziyenera kutsiriridwa! Lonjezo lirilonse lomwe Mulungu apanga limafika pokwaniritsidwa. Mbewu iliyonse ya Mulungu ndi lonjezo.

114 Ndipo, mlongo, siyani kulidula tsitsi limenelo, chifukwa ndi chinthu chosayenera pamaso pa Mulungu. Lekani kuvala zovala zimenezo, ndi themberero kwa Iye! Inu abale, inu abambo, lekani kudyetsera kwa zipembedzo izi, pa kuchita zinthu, ndi kuwalola akazi anu kumachita zinthu zoterozo. Ndi zosayenera kwa AKhristu. Bwererani ku Mawu! Atengeni Mawu awo, Iwo adzakula. Iwo ayenera kuti akule. Mphamvu ya Mulungu yosanduliza yomwe inawabweretsa Iwo apo pa malo oyamba, Iye ali basi pa ulendo Wake akubwerera, akuwatengera Iwo m'mbuyo kachiwiri tsopano. Iye ali kubwereranso komwe izo zinali.

115 Enock anakwatulidwa, kuchokera ku imfa, ndi mphamvu ya Mulungu yosintha. Kodi Mulungu anachitiranji zimenezo? Kwa choimira cha Mpingo wokwatulidwa womwe akubwera. Eya. Eliya anali mofanana. Thupi la Yesu linafulumizitsidwa ilo litafa kale. Ndipo m'manda, thupi la Yesu linafulumizitsidwa ndi Mawu a Mulungu; ndipo linasandulizidwa, kuchokera ku lakufa, fano lozizira, kukakhala Mwana wa Mulungu woukitsidwa, waulemerero. Chifukwa mneneri, Masalmo 16:10, ngati inu mukufuna kuti muzilembe izo, 16:10, anati, "Ine sindidzasiya solo Yake mu gehena, ngakhale kulola Woyera Wanga Uyo kuti awone chivundi."

O Mulungu, Mawu amenewo ayenera kuti afike pochitika, Iwo ndi Mawu a Mulungu! Adzaleni Iwo mu mtima wanu, ngati inu mukufuna kuti mudzapite mu Mkwatulo. Ngati inu mukufuna kuti mukhale AKhristu enieni, ayikenimo Mawu awa. Pamene ine ndikukhulupirira kuti anali Ezekieli, Mulungu anati, "Tenga mpukutu uwo ndipo udye iwo," kuti mneneri ndi Mawu akhoze kukhala chofanana. Ndipo lonjezo lirilonse mmenemo liyenera kuti lidzikwaniritse lokha, chifukwa ndi Mbewu yapachiyambi ya Mulungu. Musalole

munthu wina wamaphunziro azaumulungu kunja kuno kuti awatulutse Iwo mwa inu. Musamulole iye kuti apemerere pa inu ndi sayansi ya zachithupi zija ndi chidziwitso, ndi maphunziro. Zimukhulupirirani Mulungu!

116 Abrahamu sanatenge kafukufuku wamwasayansi wa tsiku lake - kuti, "Ndine wokalamba kwambiri kuti ndikhale naye mwana, ine ndapita patali kwambiri kuti ndikhale naye mwana, ine ndapita patali kwambiri. Ine ndachita ichi, icho, kapena chinacho." Koma iye anachitcha chirichonse chomwe chinali chotsutsana, ndi Mawu a Mulungu, ngati kuti panalibe. Ndipo iye sanagwedezeke ayi ku lonjezo la Mulungu, kupyolera mukusakhulupirira; koma anali wolimba ndikupereka matamando kwa Mulungu. Iye ankadziwa kuti Mulungu anali wokhaza kuti achite izo zomwe Iye anali atazilonjeza.

117 O, ana oyendayenda, olumalitsidwa ndi zoyanga za dziko lapansi lino! Alongo oyendayenda, omwe malo ndi mafashoni a dziko lino zakukopani inu! Ndipotu, mlongo wokondedwa, inu mukhoza kulingalira kuti ndine chidempete chokalamba, koma limodzi la masiku awa pamene inu mudzakomane ndi chimene Florence Shakarian anakomana nacho usiku uja; iye ankakhala mu chipinda chino, nayenso, pa malo awa, monga inu mukudziwira. Pamene inu mudzakomana nacho icho, inu mudzapeza kuti, osati ine, koma Mawu awa ndi olondola. Khalani kunja kwa nyumba zometeramo umo, masitolo a mafashoni awo. Khalani kunja kwa zinthu zimenezo.

Mukuti, "Chifukwa chiyani iwe sukumawaphunzitsa iwo zinthu zazikulu, momwe angakhalire ichi?" ingoyambani ndi ma ABC anu, ndiyeno ife tifika ku algebra, mwaona.

Ingoyambani kuphunzira, "yomwe ili ntchito yanu yoganiza bwino."

Ine ndikukupemphani inu chotero, abale, mwa zifundo za Mulungu, kuti inu mulipereke thupi lanu ngati nsembe ya moyo, yoyera, ndi yolandirika kwa Mulungu, komwe kuli kutumikira kwanu koyenera.

118 Inu muzingochita "kutumukira kwanu koyenera," Mulungu azasamalira zina zonse zakezo; mwaona, kungolingalira zinthu zomwe inu mungakhoze kuzilingalira mwa nokha ndi kuzichita. Sichoncho izo…. Kodi sichosayenera kuti mkazi adzivule yekha, ndi kumapita kunja uko ndi kumachita monga choncho, pamene Baibulo limatsutsa izo? Kodi si zosayenera kuti bambo adzikokere yekha mu mbalume zotero monga ife tiri nazo lero, ndi zinthu zonse izi pano, ndi zinthu zonse za seminare izi, ndi zinthu monga choncho, pamene ziri mwamtheradi zosiyana ndi Mawu a Mulungu? Mwaona.

119 Milomo ya Yesaya… iye anali munthu wamba chabe wa milimo yosayera. Iye anati, "Ambuye, ine ndiri pakati pa anthu osayera, ndipo ndiri ndi milomo yosayera. Watsoka ndi ine chifukwa ndamuwona Mulungu." Ndipo Mngelo anatsika, anatenga Moto, Moto Wopatulika kuchokera pa Guwa la Mulungu, ndipo anaisanduliza milomo yake; kuchokera ku milomo ya bambo oyendayenda, kukhala milomo ya mneneri wokhala ndi PAKUTI ATERO AMBUYE. Mphamvu yosanduliza ya Mulungu!

Asodzi zana limodzi ndi makumi awiri, ndi ogulitsa nsangalabwi okalamba pang'ono akazi, ndi awo omwe anadzisonkhanitsa okha mu chipinda chapamwamba ndipo anatseka zitseko, ena aiwo ali opanda maphunziro okwanira kuti alembe maina awo omwe. Mulungu anawasanduliza iwo kuchokera kwa asodzi, kukhala asodzi a anthu; kuchokera kwa amuna ndi akazi apansewu, kukakhala woyera a Mulungu, osafa. Mphamvu yosintha ya Mulungu!

120 Paulo, membala wamba wa mpingo - wa Chipresbateria, Chimethodisti, Chibaptisti, Chipentekoste, kapena chinachake; ali mu msewu iye ankapita, ndi mzimu wake wa ukulu wonyoza mwa iye, kuti iye ankadziwa zochuluka kuposa aliyense wa iwo. Iye anali atabwera pansi pa Gamalieri, m'modzi wa aphunzitsi a pamwamba omwe analipo mu dzikolo. Chinachitika ndi chiayani pa ulendo wake waku Damasiko, kukatenga gulu la anthu omwe ankakhulupirira Mawu a Mulungu? Panjira yake ya uko, anakanthidwira pansi, ndipo iye anaumva Uthenga. Ndipo Iwo unamusanduliza iye kuchokera ku membala wa mpingo ndi wopita kumpingo; kukhala mneneri wa Mulungu yemwe analemba Mawu a Mulungu, mu chipangano chatsopano. Kuchokera kumembala wa mpingo kukhala woyera!

O, nyenyezi oyendayenda, tiyeni tiime. Mwana oyendayenda, mbewu yoyendayenda yomwe ikupita kuchokera pa malo kupita kumalo, mukulumala uku; tembenukani, m'mawa uno, ana inu. Chonde ndimvereni ine - ngati munthu yemwe akuyesera kuti aime pakati pa a moyo ndi akufa.

121 Kunja uko mudziko komwe kufalitsaku kukubweraku ngati inu mukanali wolumikizidwa, inu omwe mwa yendayeda mu malo, chonde khalani mphindi yokha motalikira. Ine ndikudziwa tachedwa kuno ku Tuckson kapena, ndikupempha kukhululuka kwanu, Phoenix, ili mphindi makumi awiri kuti ikwane 12. Ndipo ine ndakhala nawo anthu awa pano mmawa onse. Ine ndakuchotsani inu kutchito yanu ndi zinthu. Koma taonani, mzanga wokondedwa, inu mukhoza kukhala muli kutali ndi Mulungu kwa nthawi zonse. Chonde bwererani m'mawa uno. Mungatero inu? Pali malo pakasupe.

Modyetsera ng'ombe kale, izi ndi zoona,

Mwana anabadwa kudzawapulumutsa anthu

Ku tchimo lawo.

Yohane anamuwona iye pa gombe

Mwana wa Nkhosa nthawizonse

O, Khristu, wopachikidwa pa Kalvare.

O, ndinkonda mwamuna wa ku Galileya, wa ku

Galileya,

Iye wandichitira zambiri ine.

Wandikhululukira machimo anga onse,

Nayika MzimuWoyera;

O ndankonda o ndakona, mwamuna wa ku Galileya.

Wamisonkho anapita kukapemphera

tsiku lina Mkachisimo,

Anafuula, "O Ambuye, ndichitireni chifundo ine!"

Anakhululukidwa tchimo lonse namupatsa

Mtendere wozama;

Anati, "Idzani muone mwamuna wa ku Galileya."

Zoona.

Wolamula anayenda, mbuu anayankhula,

Mphamvu ija inayankhula mwachikondi pa Nyanja;

Wakhungu anawona, ndikudziwa zinatheka

Ndi chifundo cha mwamuna uja wa

Fanizirani izo ndi utumuki lero.

Mkazi wapachitsime, iye anamuuza

Machimo ake onse,

Mmene iye anakhalira ndi amuna asanu panthawiyo.

Anankhululukira tchimo mtendere ozama Unadzamo;

Anafuula, "dzawoneni mwamuna wa ku Galileya!"

122 Mkazi, Iye akhoza kuchita zofanana. Iye wawerenga mtima wanu mmawa uno bambo, Iye wauwerenga mtima wanu. O, wansonkho, tiyeni tipemphere!

O, ndinkonda mwamuna wa ku Galileya, wa ku

Galileya,

Iye wandichitira zambiri.

Wandikhululuiira machismo anga onse, nandipatsa Mzimu

Woyera,

O, ndinkonda, ndinkonda mwamuna wa ku Galileya.

Kodi inu simumukonda iye, ndi ine, m'mawa uno? O, wochimwa wa mphepete mwanjira, oyendayenda, kuno kapena kwina kumene inu mungakhale muli, kodi inu mungamulandire Ambuye wanga mmawa uno? Iye ndiye Mawu, ndipo Mawu abweretsedwa kwa inu. Kodi inu simumulandira Iye m'mawa uno? Kodi inu mungangokweza manja anu kapena kuima pamapazi anu, kapena chinachake, ndikupemphera, mudziti, "Ine ndikufuna kuti ndi mulandire Iye pakali pano. M'bale, ine ndi kulolera. Ine ndikufuna pakali pano kuti ndimuvomereze Iye." Kodi inu mungaime pamapazi anu, aliyense yemwe akufuna kuti apemphereredwe, ndikuti, "Ine ndiri …." Kupemphereredwa, kani, "Ndine wochimwa. Ine ndikufuna…." Mulungu akudalitseni

inu, bwana. Winawakenso? Aliyense zipempherani tsopano, mphindi yokha.

Modyetsera ng'ombe kale, (Ilo linali mu

Chisokonezeko, inu mukudziwa, dzikoli

Linali), ndipo ndikudziwa izi ndi zoona,

Mwana anabadwa kudzapulumutsa anthu kutchimo lao.

Yohane anamuwona pa Gombe,

Mwanawankhosa nthawizonse, (Iye yemweyo lero)

O, Iye ndi Khristu, wopachikidwa pa Kalivare.

123 Kodi inu simumukonda iye ndi mtima wanu wonse, chotero inu mukhoza kuchoka kuchikhalidwe cha dziko ichi chomwe inu mwakhalamo? Inu akazi, inu abambo, o, kodi inu munakhalira chiani pano pa nthawi yonse iyi? Izo zikusonyeza kuti pali chinachake pansipo mwa inu, muli chinachake umo chikumva njala ndi ludzu. Inu simukanati mukhala pano ma ora awiri kapena atatu awa, kukhala mu nyumba ino monga chonchi; pali china chake. Kodi simuti mungomvetsera kwa icho lero? Mulole ma fashoni ndi sayansi, ndi zinthu zonse za dziko, zichokemo mu malingaliro anu pakali pano, m'bale wokondedwa kapena mlongo wokondedwa.

Mipingo ikuyanjana, mafuko akulu ali

Kusweka Israeli akuuka,

Zizindikiro zomwe aneneri ananeneratu;

Masiku a amitundu atha, ndi zoopsya

Zitachuluka;

“Bwererani, omwazika inu, kwa inu eni.”

Tsiku la chiwombolo layandikira

mitima ya anthu ikulephera mwa mantha;

Dzazidwani ndi Mzimu, nyali zanu ziwale

Yang'anani mmwamba chiwombolo

chayandikira!

Aneneri abodza akunama, Choonadi cha

Mulungu akuchikana,

Kuti Yesu Khristu ndi Mulungu.

124 Tsopano izo ndi zoona. Inu mukudziwa zimenezo, tonse ife, tsiku limene ife tiri kukhalmo.

Koma Iye anati kudzakhala kuwala nthawi ya madzulo,

Njira ya ulemerero inu mudzaipezadi.

Ndilo tsiku limene ife tiri nkukhalamoli pakali pano. Kuwala kudzawala cha mu nthawi ya madzulo pamene mdima ukubweramo, nthawi yakuwala kwa chizirezire, nyenyezi yakumadzulo.

Kuwala kwa chizirezire ndi nyenyezi

ya usiku,

Pambuyo pa uko mdima!

Kudzakhala kulibe chisoni cha kutsazikana,

Pamene ine potsirizano ndi dzauyamba;

Pakuti zonse zakunja ziri ndi nthawi ndi

Danga,

Ndipo mafunde akhoza kutengera ine

Kutali,

Koma ndikufuna ndidzamuwone

Ondiwongolera wanga maso Ndi maso

Pamene ndidzawoloka mu chonchinga.

Musandiuze ine, ndi nyimbo za chisoni,

Kuti moyo uli loto chabe lopanda kanthu!

Ndipo moyo uliwa kufa umene wagona,

Ndipo zinthu siziri momwe izo

Zimawonekera.

Eya, moyo ndi weniweni! Ndipo moyo ndi

Wotsimikizika!

Ndipo manda simathero ake;

Pakuti fumbi iwe uli, kufumbi udzabwerera,

Sizinali kuyankhulidwira za moyo.

Miyoyo ya aamuna aakulu onse

Imatikumbutsa ife,

Ndipo ife tingaipangitse miyoyo yathu

Mwapamwamba,

Ndipo, posiyana, kutisiyira mbuyo mwathu,

Mphondero munchenga mwanthawi,

Mphondero, kuti mwinamwake

Winawake,

Ali nkuyandama munjira ya moyo wokwiya,

M'bale wosimidwa ndi wangalawa

Yophwasuka,

Pakuwona, adzagwire mtima kachiwiri.

Tiyeni tigalamuke, ndiye, ndi kumachitapo,

Ndi mtima pakulimbana kulikonse;

Musakhale ng'ombe yosalankhula,

Yodudulizidwa!

Khalani ngwazi mukulimbana!

125 Wokondedwa Mulungu, awa ndi anu. Ine ndawawona amuna awiri aimirira pamapazi awo, Atate. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti inu muwatenge iwo tsopano. Iwo akufuna kuti akhale ana anu. Iwo awuka kuchokera kuumbuli wa moyo umene iwo aukhala, ndipo tsopano iwo akufuna akhale otsitsimusidwa, mwatsopano, ndi ubatizo wa Mzimu Woyera pa mbewu iyo yomwe yabzalidwa mmitima yawo tsiku lino. Mulungu wamuyaya, mlengi wazinthuzonse, yemwe munapanga Mawu Anu, ndipo ine ndikukhulupirira kuti inu munkadziwa kuti amuna awa akanati achite izi mmawa uno. Ine ndikupemphera, Ambuye, kuti inu muwatsirire Mawu awo, usana ndi usiku, ndipo musamulore konse Satana kuti awakhwatule iwo kuchokera m'manja mwanu. Mulole iwo ukakhale mtengo umene nthawi ina, mu Paradiso wa Mulungu, pamene zonse zidzabweretsedwa kachiwiri.. Pakuti Mawu anu sangakhoze kulephera. Izo zidzakhoze kukhala kachiwiri kwa dziko lino….

126 Ndipo sipadzakhala pali chitukuko cha mtundu uwu mu dziko likudzalo. Kudzakhala kulibe magalimo kapena kalikonse komwe sayansi inayamba yapangapo. Kudzakhala kulibe zinthu zoterozo mu dziko

likudzalo. Koma chidzakhala chiri chitukuko cha mtundu wa Mulungu womwe chomwe Iye ati adzachikhazikitse mu ulamuliro wa ulemerero. Pakuti, muchitukuko ichi muli matenda, imfa, zisoni, manda, ndi zosowa. Koma mu ufumu uwo womwe uli nkudza uko kulibe imfa ayi, kulibe zisoni, kulibe matenda, kulibe usinkhu wa ukalamba. O Mulungu, zonse zidzakhala ziri zatsopano uko, muchitukuko chanu. Mulungu, tisintheni ife lero, ndi mphamvu yanu, mwakusintha kwa malingaliro anthu, kuti tichoke kuzinthu zoperewera za dziko lino, kupita ku Mawu a Mulungu. Ndipo mulole ife tikonzedwenso ndi mphamvu yosintha ya Mulungu pa mbewu yomwe iri mu mtima mwathu, pakuti ife tikukhulupirira, mpaka kuzolengedwa zotchedwa ana a amuna ndi a akazi a Mulungu. Ili ndipemphero langa kwa inu, Atate, chifukwa cha anthu, mu dzina la Yesu. Ameni.

127 Tsopano kwa inu muli kunja kofalitsidwira, kulikonse komwe inu muli, ine ndikufuna kuti inu mulandire Khristu uko komwe, ngati mpuliumutsi wanu wanu, ndikuti mudzadzidwe ndi Mzimu Wake. Mawu omwe anenedwa mmawa uno, mulole iwo agwere mu mtima mwanu ndipo mulole apo inu mumulandire Yesu.

Ndipo muupenye moyo wanu, ndipo muone chomwe inu muzikhala pa mbuyo pake. Ndipo mutenge Sefa ya mwamuna woganiza pano. Pamene inu mudziwona nokha mukuchita chinachake chomwe chiri chosiyana ndi Mawu awa, muzisuntha kuchoka kwa icho, mwansanga kumene. Mwaona? Chifukwa, pali sefa yomwe imatchingira imfa kutali ndi inu, awo ndiwo Mawu a Mulungu. Mawu Ake ali Moyo, ndipo iwo azikutetezani inu ku imfa.

128 Anthu inu pano omwe muli nyumba yoyankhuliramoyi, ine ndakhala nanu inu muno kwa nthawi yayitali. Ine ndikukuthokozani inu chifukwa chakukhalapo kwanu. Ine ndikupempherani kuti Mulungu asadzalole konse kuti mbewu iyi ife. Ine ndikuyembekeza inu simukuganiza kuti ine ndaima pano kungoti ndinene zinthu izi kuti ndikhale wosiyana. Ine ndinazinena izo chifukwa cha chikondi; ndiodziwa kuti pamene ine ndiri muthupi lakufa ili, monga ine ndiliri tsopano ndi nthawi yokhayi yomwe ine ndidzakhoze konse kumalalikira kwa anthu. Ndipo ine ndimamukonda Yesu Khristu. Iye ndi Mpulumutsi wanga.

Ndipo kumbukirani ine ndikanakhala ndiri kunja uko kumsewu ngati akanati asakhale Iye. Ine ndikanakhala ndiri kunja uko; makolo anga onse, abale anga onse, anali wochimwa. Koma Mulungu, ndi mphamvu Yake yosintha, ine ndikudziwa iyo inandipananga ine kukhala cholengedwa chosiyana mwa ine. Ndipo ine ndikhoza - ine ndikhoza kuchitira umboni kwa inu, kuti ndiyabwino. Ndipo iyo idzakusungani munthawi ya mavuto. Ngakhale pa imfa, ili pakhomo, inu mulibe mantha. "Palibe chomwe chingatilekanitse ife kuchikondi cha Mulungu, chomwe chiri mwa Khristu." Mulole Mulungu adalitse aliyense wa inu, ndikukupatsani inu Moyo wa Muyaya.

129 Ndi angati muno womwe alibe mbewu ya Mulungu, ubatizo wa Mzimu Woyera? Kodi inu mungangokweza dzanja lanu, ndikuti, "Mundikumbukire ine, m'bale Branham, kuti ine ndiulandire Mzimu Woyera uwu." Tsopano muwatengere Mawu mkati mwanu - mumtima wanu, ndikuwakhulupirira iwo. Tsopano ngati inu…mukhoza kuyang'ana pa inu. Mupite uko ndikukadziyang'anira pa kalilole, ndipo inu mukhoza kuwona pomwe inu muli. Mwaona, inu mukhoza kudziwa. Inu mukuti, "chabwino, ine sindinakweze dzanja langa, chifukwa ine ndikukhulupirira kuti ndiri nawo." Dziyang'anireni nokha mu kalilole ndiye inu muwona mtundu wa mzimu womwe ukukunyengani inu, mwaona.

Kunyengedwa, kuganiza… "Pali njira yomwe imawoneka yolondola kwa munthu, koma mathero ake ndi njira ya imfa." Kodi izo nzoona?

Pammtanda mpulumutsi anafa,

Kunditsuka tchimo ndinalira;

O, magazi anatsuka mtima wanga;

Ulemerero…

130 Ingotsekani maso anu, phindi tsopano, ndikumangoimba iyo kwa Iye tiyeni tingokwezera manja athu m'mwamba.

Ulemerero kwa dzina, Lake lofunika!

Ulemerero kwa dzina Lake

Magazi anapakidwa pa mtima wanga;

Ulemerero kwa lake….

Ine ndikufuna inu aKhristu kuti mugwirane chanza wina ndi nzake, yemwe ali wopulumutsidwa.

Ndapulumutsidwa modabwitsa,

Yesu akhala mkati mokoma,

Pamtanda anandilowetsamo;

Ulemerero kwa dzina Lake!

Ulemerero kwa dzina Lake Lofunika!

Ulemerero kwa dzina Lake!

O, magazi anapakidwa pa mtima wanga;

Ulemerero kwa dzina Lake!

131 Magazi ali ndi nyongolotsi ya Moyo mwa Iwo, inu mukudziwa. Izi ndi za kwa iwo omwe sakumudziwa Iye.

O, bwera ku kasupe okomayo;

Gwetsera moyo pa mapazi ake;

O, gweramo, ukhale wa phumphu;

Ulemerero kwa dzina Lake!

O, ulemerero kwa….

Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano pamene ife tikuiimba iyo.

Ulemerero kwa dzina Lake!

Magazi anapakidwa pa mtima wanga;

Ulemerero kwa dzina la Lake

132 Inu mukumukonda Iye? Paulo anati, "Ine ndiziimba mu Mzimu. Ine ndidzipembedza mu mzimu."Tiyeni tiimbe iyo mofewa kachiwiri. Ndi manja athu mmwamba. Inu mukudziwa, vuto lake, ife anthu achipentekoste, ife tataya Chimwemwe chathu, ife tataya kutengeka kwathu, monga Billy Graham ananena usiku wina, "Alaliki awa, otembenuza makolala, akupita kumwera uko, akuomba mmanja mwawo, ndi kudumphadumpha pa mapazi awo panthaka, ndikumamenya, iwo anali ndi china chake chomwe iwo ankakondwera nacho." Chabwino, eya, ine ndiri ndichina chake chomwe ndikukondwera nacho. Mwaona. Eya, ife tataya kutengeka kwathu. Tsopano tiyeni tingokweza manja athu. Musadandaule nayo misozi, iyo sipweteka chiri chonse, onani. Iyo sipweteka. "Iye amene amapita kwina akufesa, mwa misonzi, mopanda kukaika adzabwerera kachiwiri, akubweretsa zipatso zofunikira." Chabwino.

Ulemerero kwa dzina lake lofunika!

Ulemerero kwa dzina lake!

Magazi anapakidwa pa mtima wanga;

Ulemerero kwa dzina lake!

Ulemerero kwa dzina lake… (O Mulungu!

Mulungu alemekezeke!)

Ulemerero kwa dzina lake!

Titimiritsani mbewu, Ambuye, mumtima!

Magazi anapakidwa pa mtima wanga;

Ulemerero kwa dzina lake!

Maulaliki wolalikidawa ndi

William Marrion Branham

"...mu masiku a liwu..." Chivumbulutso 10:7

www.messagehub.info